


LAWRENCE KADZITCHE

KATAKWE



M'DZINA LA YESU

M'DZINA LA YESU

LAWRENCE KADZITCHE

All rights reserved. No part of this book may be
reproduced, stored in a retrieval
system, or transmitted in any form or by any means,
electronic, mechanical,
photocopying, recording, or otherwise, without the
prior written permission of the
copyright owner

Copyright: Lawrence Kadzitche 2020

Illustrations: Raphael Mawera

Design: Kondwani Kamiyala

Nkhaniyi ndiyopeka. Maina, anthu, malo kapena
zochitika ndizopeka kapena
zikugwiritsidwa ntchito mwanthano ndipo ngati
zikufanana mwa njira ina iliyonse
ndi anthu enieni, amoyo kapena akufa, zochitika
zenizeni kapena malo enieni, izi
ndi zongofanana chabe.

Again, for Martha Kadzitche

“Pomwepo munthu akanena kwa inu, onani Khrisitu
ali kuno, kapena uko musamuvomereze; chifukwa
akrisitu onama adzauka, ndi aneneri onama
nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa: koter
kuti akanyenge, ngati nkotheka, osankhidwa omwe.
Onani ndakuuziranitu pasadafike.”
—Mateyu 24: 23-25

ZA MKATIMU

Mutu	Tsamba
1. Mbusa Kaduya	1
2. Dzanja la Mulungu	6
3. Mayesero a Satana	10
4. Mpingo Uyamba	15
5. Chozizwitsa Choyamba	19
6. Njoka Yokalamba	23
7. Mpingo Ukula	30
8. Mphwanu ndi Big	35
9. Mayendetsedwe a Mpingo	40
10. Chonyansa Pamalo Oyera	50
11. Ahabu ndi Yezeberi	55
12. Satana Aonetsa Nkhope	62
13. Chiwanda Chowopsa	66
14. Nkhope ya Mulungu	69



Mbusa Kaduya

Kugogoda ndikomwe kudamudzutsa Katakwe. Adazindikira kuti adagona ndi zovala mthupi komanso osafunda. Adaponya miyendo yake pansi, nayasamula kenaka nkudzungola. Mokwiya, adakupiza ntchentche yomwe inkafuna kuwulukira mkamwa mwake.

Kwa kanthawi, adakhala pabedipo atagwira mutu wake womwe umamuwawa kaamba kamatsire. Mnyamata wazaka makumi atatu, adali wamsinkhu wapakatikati. Mutu wake udali waukulu chipumi ndipo udanka nutepa ngati nguli nkukasongokera kuchigama chofoleredwa ndi ndevu zatonde. Ngakhale sadali wonenepa, mimba yake idali yamtsuko ngati yanthumbidwa chifukwa chamowa.

Adaimirira, nkudzungolando kangapo. Kenaka adasansa makwinya a sikipa yake yolekeza mkhosi ndi kuongolando buluku lake lafuleya la tchekitcheki. Nsapato yake yakuda yosongoka idali psu ndi katondo. Adatola kachipewa kake kakapusi komwe sikamachoka kumutu nkuyenda monyinyirika kukatsegula chitseko.

Kunjako kudaima John Kaduya, mnyamata yemwe amakhala mu limodzi mwa makomo asanu a mdadadawo. Udali mdadada woti munthu woyamba kuwuona kumene akhoza kuganiza kuti ugwa nthawi ina iliyonse. Makoma adali ndi ming'alu paliponse. Mphepo inkalephera kuyalula malata chifukwa cha miyala yomwe idaponyedwa padengapo.

Makomo onsewa ankagwiritsa ntchito chimbudzi chopanda denga chomwe chitseko chake idali nsalu yachipani yong'ambika. Nalo bafa lidali limodzi- kanyumba kogumuka koti munthu amafunika kumasamba chowerama kuti asaonekere kuchokera mchiuno kupita kumutu.

“Kodi ndi abusa!” Katakwe adatero akuipitsa nkhopre ngati wavumata chivululu chifukwa cha mutu unkamupweteka uja.

Kaduya adali ndi utumiki wachipentekosite womwe amapangira pansi pamtengo wina wapafupi ndi mdadadawo. Mamembala a utumikiwo adali akuti munthu akhoza kuwawerenga ndizala zadzanja limodzi.

“Ndinetu, mtsogoleri,” Kaduya adayankha. Pokhala amsinkhu umodzi komanso ochezerana momasuka, iye ankamutcha Katakwe

“mtsogoleri” ngakhale kuti Katakwe sadali membala wamphingo wake. “Ndinadabwa duwa likukwera neba osadzuka ndati nthawi zina umangoti munthu akugona apo atachitika ogo.”

Katakwe adayang’ana kumwamba. Dzuwa lidali paliwombo. “Kungoti dzulo ndinaupsipsintha bad ku Chigwiri moti ndafika mbandakucha.”

“Dzulo pokhala Lachisanu, nanenso ndinaganiza choncho, mtsogoleri,” adavomereza Kaduya.

Thukuta lidatsika pankhope ya Katakwe. Tsikulo kudatentha kwambiri, zomwe zidali zodabwitsa mmwezi wa Juni. Kupatula makwangwala omwe ankauluka, kumwamba kudali biriwiri kopanda ndi mtambo womwe. Katakwe adakamula thukutalo ndi dzanja lamanja.

“Eee, njala ndiye yanding’amba bwanji,” iye adabuwula, akugwira mimba yomwe mkatи mwake munkabangula mabingu. “Dzulo ndimangouluma osadyera.”

John Kaduya adaponya diso lake pa Katakwe nagwedeza mutu wake mwachisoni. “Atsogoleri, kumwa mowa ndikuchimwa ndipo mphotho yauchimo ndi imfa. Landirani Yesu...”

“Ndiye ndikhuta Yesuyo?” Katakwe adamutsekereza.

Kaduya adapukusa mutu wake nadzuma. “Chabwino, tiye mnyumba tikadye.”

“Apo ndiye ukulankhula, munthu wa Mulungu,” Katakwe adabwekera akumulondola mbusayo mnyumba. Adapeza mbale zili patebulo. Iye sadazengereze; akuti azisamba mmanja, Kaduya adamugwira dzanja. “Tiyamike kaye, atsogoleri.”

“Our Heavenly Father, we thank you for the banquet we are about to partake. Please bless this food and those who have prepared it. We also ask for special blessings for those who are in need of food so that they may find it. In Jesus’ name we have prayed. AMEN,” mbusayo adapemphera mchingerezi monga amakondera abusa achipente.

“Amen,” adayankha Katakwe.

Kaduya adavundukula mbale. Nkhope ya Katakwe idasintha ngati akuona mzukwa. Mmbalemo mudalibe kena kalikonse. Adamugenda mbusayo ndi diso lodabwa.

“Mtima wako usavutike, neba,” Kaduya adapereka yankho kufunso losafunsidwalo. “Lero mmbalezi mulibe chakudya koma tsiku lina Mulungu adzatipatsa chakudya chokwanira oti tizidzadyetsa ena,” adadukiza namugwira Katakwe padzanja. “Mulungu wathu ndi Mulungu wa ma miracles-wazatheka bwanji. Mulungu adzatipatsa chinyumba ndipo pakona ngati iyi padzakhala TV, iyi wailesi, apa sofa.”

Katakwe adalephera kupilira ndipo adagwa nalo phwete. “Amwene, mmalo moti muzigwira ntchito muzingokhalira kunenera kuti Ambuye adza...li limenelo?”

“Mulungu safulumira kapena kuchedwa; panthawi yoyiikikayo adzandipatsa,” adalimbikira Kaduya.

“Akulephera kukupatsani nsima ndiye nkudzakupatsani nyumba?” adafunsa Katakwe. “Yaubusa iponyeni pansi ikuchedwetsani, mani.”

“Iyitu sintchito koma maitanidwe,” Kaduya adaunikira. “Chomwe ndikudziwa nchoti Mulungu salola atumiki ake avutike.”

Katakwe adasekanso. “Ndiye Mulunguyo adzachita kugwetsa zinthuzo kuchokera kumwamba?”

“Njira zoperekera za Mulungu zimakhala zodabwitsa. Aizraeli adawagwetsera mana mchipululu, Eliya adamudyetsa ndi makungubwi...”

“Ndiye inu *mansion* idzachita kugwa kuchokera kumwamba?” Katakwe adamudula mbusayo. “Utumiki ungokusaukitsani, mani, tiyeni tizikangofuna maganyu mtauni.”

Kaduya adaoneka kuti izi sizidamugwetse mphwayi. “Izi mpang’ono chabe,” iye adatsimikiza akumukokera Katakwe panja. “Panopa ndikupita wapansi mtauni, koma tsiku lina ndidzapita pagalimoto.”

Monga akuchita zisudzo, mbusayo adakhala ngati akulowa mgalimoto, adatseka chitseko, nkuliza motikaleyo kenaka nkuiponya mgiya. Adanyamuka.

“Amwene, nthawi iliyonse mulowa mtchire basi!”

“Ukuiona bwanji mothia andipatsa Ambuyeyi?”

Katakwe adakweza manja. “Uwu ndi msala basi.”

“Vuto lako Katakwe ndilakuti ulibe chikhulupiriro, sukhulupirira kuti ndi Mulungu chili chonse nchotheka, amatenga kapolo

kukhala mfumu,” adafotokoza Kaduya. “Chomwe ndikuchita pano ndikumanga mzimu wa umphawi ndikulengeza madalitso omwe Ambuye adzandipatse.”

Katakwe adaponya diso lake pa Kaduya. Munthu wa Mulunguyo ankasunga tsitsi lambiri mokopera abusa ena otchuka omwe ankachitanso chimodzimodzi. Koma kusiyana ndi abusa otchukawo, iye adali msuti yosoketsa yobiriwira yomwe idali itayamba kusintha mtundu kulowera kumtundu waudzu wofota. Wamtali ndi woonda, zovalazo zinkangokhala ngati azipachika pachothamangitsira anyani kumunda. Nsapato yake idali itayamba kuyasama monga chambo chouma.

“Inuyo mudzakhala ndi nyumba ndi galimoto?” adafunsa Katakwe ndi mawu okutidwa ndi kuderera.

“Eya.”

“Motani?”

“Sikuli kwa ine kudziwa koma Yehova adzadziwa njira yake. He feeds and clothes birds what about me his servant?”

“Zikadzachitika, udzandidule chala ichi,” Katakwe adalumbira akusonyeza chala chake cholozera.





Dzanja la Mulungu

Lokeshoniyo chidali chisa cha njuzi-tinyumba tambirimbiри tomangidwa mopanda pulani. Mudali nyumba zanjerwa, zadothi, zaudzu, zamalata- zonse zongomangidwa pomwe ndi momwe mwini wake amafunira. Padalibe malo otaya zinyalala, motero paliponse padali padzala. Fungo loipa silinkachoka monga muja kumakhalira kumtaya. Padalibe msewu wokonzedwa kuti uwu ndi msewu, misewu idali mipata yomwe inkasiyidwa ndi nyumbazo bola ngati galimoto ingadutse.

Adalipo magalimoto awiri. Patsogolo padali Prado ndipo inkatsatidwa ndi Mercedes Benz. Magalimotowo ankakwawa kaamba koonongeka komanso kuchepa kwa msewuwo.

Magalimoto apamwamba sakhalā chinthu chooneka tsiku lililonse mulokeshoni motero khamu la ana linkawathamangira osasamala fumbi lomwe magalimotowo amamwaza.

Izi Katakwe adaziona kuchokera pakhonde lamdadada ankakhala uja. Anadabwa pomwe ulendo wamagalimotowo udadzathera panja pamdadawo. Dilaivala wa Prado ija adatsika nkukatsegula chitseko chapasenjala.

Munthu wamfupi ndi wonenepa adatsika. Chilichonse chamunthuyo chimaonetsa ndalamā, kuchokera kusuti yake yakuda mpaka kunsapato zake zakuda zang'aning'ani. Yemwe adatsika mu Benzi ija amaoneka kuti adali dilaivala chabe.

Mai a Nsikwa, omwe amakhala khomo loyambirira, sadaikireko nzeru kwa alendowo; adangopitiriza kuchapa. Anyamata awiri ogulitsa makala omwe amakhala khomo lachiwiri adali atachokapo. Jintukesi, yemwe amakhala khomo lachitatu adalipo-koma naye adangopitirira kusuta chingambwe osalabadira za magalimotowo. Katakwe amakhala khomo lachinayi ndipo John Kaduya ndiye amakhala khomo lomaliza.

Katakwe, yemwe adagona motsamira khoma, adagugudiza botolo la kachasu lomwe ankamwa nkuliponya uko. Adaipitsa nkhopē kenaka nkugeya mokhutitsidwa. Adatola kachipewa kakapusī komwe kadali pakhundu pake nkutsomeka kumutu. Adaimirira nayenda monjanja kulunjika padaima magalimoto aja.

“Wawa, bwana,” iye adalonjera mkulu adali msuti uja.

“Tikuthandizeni?”

“Eya, odala. Niluwunguza obusa,” adayankha mkuluyo mchichewa cha ku Nkhoma ku Lilongwe.

Katakwe adadzidzimuka. Adamuyang’ana mkuluyo modabwa. mudzina.

Munthu wandalama ngati ameneyo amafuna chiyani kwa munthu waulesi yemwe amanamizira kuti ndi mtumiki wa Mulungu uja?

“Abusa? Abusa ake ati?” iye adafuna kumvetsetsa.

“Dzinalanizemba. Koma pano sipali obusa ena ake omwe odavuchitira mapemphero patsinde pamtengo uwo?” mkuluyo adafunsa akuloza chimtengo china chake chowwandamuka cha senderera.

“Ndawadziwa,” Katakwe adatero. “Dikirani ndiwaitane.”

Katakwe adathamangira pakhomo la Kaduya. Adangofikira kulowa osagogoda. Adamupeza mbusayo akuwerenga baibulo.

“Amwene, sindikudziwa kuti mwapalamula chiyani, koma pali mchikumbe wafodya akukufunani panjapa,” Katakwe adafotokoza monyoza.

“Atsogoleri, osamalankhula mwachipongwe za alendo mudzanyoza angelo,” Kaduya adamuchenjeza.

Katakwe adaseka. “Angelo nkuyendera inuyo?” adadukiza, namwaza maso mnyumbamo. Katundu adali tebulo ndi mipando yathabwa inayi. Kenaka adamuyang’ana Kaduya. Suti yake yobiriwira ija tsopano imaoneka ngati udzu nthawi yachilala pomwe nsapato yake idali itayasama ngati chimbano. Tsitsi ankasunga lambiri lija lidali lofyira kaamba kosowa mafuta osamalira tsitsi. “Ndiliti lija mudayamba kunenera kuti Ambuye adzakuyenderani?”

“Ambuye amachita zonse munthawi yake-safulumira, sachedwa,” adalongosola Kaduya akutuluka mnyumbamo.

Katakwe adamutsatira mbusayo kubwerera pomwe padaima alendo aja. Akuyandikira, mkulu wasuti uja adatambasula manja ake nkumukumbatira Kaduya muja amachitira anthu oti asowana nthawi yaitali.

“Nakonjwa kukupenyani, mnthu wa Chauta,” mkuluyo adatero. “Mwankumbukira?”

Kaduya adamuyang’ana mkuluyo. Adaonetsa kuti sadamuzindikire.

“Simungankumbukiredi. Naona kuti nhkale ochimwenewa odzu unizindikira,” munthuyo adatero akuloza Katakwe ndi mutu. “Ndine Sofiasi.”

Katakwe adadzidzimuka. Sofiasi adali mkulu wina yemwe ankachita bizinesi yansomba ndipo amakonda kubwera kudzapemphera zaka ziwiri zapitazo. Pomwe nthawiyo adali wochepa thupi ngati udzudzu panopa adali wofufuma mosasiyana ndi finye.

“Obusa, paja nyengo ime ija ninkati muzinipempherera kuti bizimezi yanga iyende bwino,” adapitirira Sofiasi. “Ambuye odalandi mapemphe anu, mnthu wachauta.”

Katakwe adali asadamuonepo Kaduya atadabwa ngati momwe anadabwira nthawi imeneyo.


“Moti panopa zinthu ziluyenda bwino kwankwene. Nili ni bizimezi ya magolosale, vigayo ni vimamotikale vonyamu katundu,” adalongosola Sofiasi. “Ndiye nabwevuka kuti nidzathokoze.”

Pamalopo padagwa bata ngati kuti aliyense akufuna kumva kuti mkuluyo athokoza mwamtundu wanji. Galu yemwe adagona pansi pamtengo adadzutsa mutu. Nkhuku zomwe zimapalapasa padzala zidaima kaye. Ngakhale mbalame zimene zidasiya kuimba. Gulo yemwe adali pamwala adadzutsa mutu.

“Obusa, anga njira yokuthokozerani komanso kupyitsa patsogolo utumiki wa Chauta, nakugulirani motikale iyi,” Sofiasi adatero akuloza benzi ija.

Katakwe adati kukamwa yasa. Sofiasi sadaimire pomwepo. “Komanso nakugulirani khumbi ku Area 47.” Katakwe adagwira pakhosи ngati watsamwa-maso ali tuzu, kukamwa kuli pululu. “Apa musalowenso mnyumba-katundu wamnyumba nakugulirani kale, basi tifumuke koma tikhwetera kaye mtauni nikakugulireni mbota.”

Katakwe adamva chizungulire. Mdima udamukuta ndipo adagwa pansi.





Mayesero a Satana

Malaya a Katakwe adamatirira kumsana, thukuta likutsika ngati misozi kaamba kakutentha omanso mtunda womwe adayenda. Adayang'ana kumwamba. Sadaone mtambo ngakhale umodzi.

"Koma kutentha kumeneku ndi kwamtundu wanji mwezi uno wa Julaye,"

Katakwe adadzilankhulira akupukuta thukuta lija ndi kathaulo. "Kapena ndikusintha kwa nyengo akunena azanyengo kuja."

Adafika panyumba yomwe amafuna. Adaima kaye kuti mtima ukhale mmalo. Kenaka adagogoda. Geti lidatseguka ndipo mlonda ali mu unifomu yakuda adaonekera.

"Tikuthandizeni?" adafunsa mlondayo.

"Eya," adavomera Katakwe. "Ndikufuna ndionane ndi abusa a Kaduya."

Mlondayo adamuyang'ana Katakwe momukweza ndi kumutsitsa ngati akuyang'ana chiweto choti chili pamalonda. "Muli ndi appointment?"

Katakwe adaponya diso lake pa mlondayo monyansidwa. Kodi mgwanyayo samadziwa kuti mwezi watha womweyu mbusa adali bwana wakeyo amagona ndi njala pomwe iye Katakwe amakhala akuchezera kumwa mowa kumabala?

"Mungoti kwafika Katakwe."

Nkhope ya mlondayo idawala. "Pepani, bwana, sindinakuzindikireni. Anandiua kuti mufika kungoti sindimaganiza kuti ndinu. Tiyen ndikuperekezeni."

Adalowa mkaati mwa mpanda. Maso a Katakwe adagwa panyumba yaikulu yozunguliridwa ndi kapinda wosamaliridwa bwino. Kafungo kabwino kadachokera mmaluwa okongola omwe adali apo ndi apo. Mercedes Benz ija idaimikidwa kumaso kwa nyumbayo. Mlondayo adamupereka kwa wantchito yemwe adavala yunifomu yoyer ya ukhukhi. Katakwe adatsagana ndi khukiyo ulendo mnyumba.

Adapeza Kaduya akumudikira m'chipinda chochezera. Pang'onong'ono Katakwe sadakamuzindikira mbusayo-adali atasintha chilichonse. Tsitsi lake tsopano lidali lakuda ndi lothiridwa bwino mafuta. Adali msuti yofiyira ndipo nsapato zomwe zidali kuphazi

zidali zofiyiranso. Shati yomwe adavala idali yoyerwa ngati matalala. Pamkono padali wotchi yodula.

“Welcome, Katakwe,” Kaduya adatero akumukumbatira. “Take a seat.”

Chipindacho chidali chokongola modabwitsa. Makoma adali opetedwa bwino ndi penti yokongola yachikasu. Masofa awiri apamwamba adazungulira katebulo ka galasi. Pakona imodzi padali TV yomwe panthawiyo inkaonetsa mlaliki wina wotchuka wa ku Nigeria akupantha uthenga. Wailesi yomwe idali mnyumbamo idali yaikulu ndi yapamwamba kwambiri.

“Ndikupatseni chakumwa chanji, atsogoleri?” Kaduya adafunsa.

“Katakhala ka *brandy* simungalakwitse,” adayankha Katakwe.

“Kukhosiku kwangoumiratu.”

Kaduya adaseka. “Mbusa wamtundu wanji angamasunge chakumwa chadyabulosi m’nyumba mwake? Pajatu ine sindikhudza chakumwa chaukali ngakhale ndi ndodo yaitali.”

“Ndimati mwina mumakhala ndikena kake kakuseri kwa bedi koyeretsera mmaso mukamapita kuguwa,” Katakwe adayankha moseka.

Kaduya adagwedeza mutu. “Vuto lako Katakwe ndilakuti umazitenga zinthu za Mulungu mwachibwana. Adakakhala masiku akale Mulungu adakakhala atakukantha kalekale.”

Mumtima Katakwe adati bwanji sakuantha iweyo wonamizira dzina la Mulungu koma pamaso adati, “Chabwino ingondipatsani Coca Cola.”

Adamubweretsera chakumwacho ndikumuthirira mu tambula ya galasi.

“Munthu wa Mulungu, apa ndiye mwafika,” Katakwe adayamikira kwinaku akumwa Coca Cola uja. “Chinyumba chabwino, mlonda pageti...”

“Mulungu wathu ndiwabwino, achimwene,” adavomereza Kaduya.

“Amasamalira atumiki ake.”

“Munthu wa Mulungu, amati nzeru nzayekha adavyiyika nsima mmadzi,” Katakwe adatsitsa mawu. “Zakuchitikirazi zanditenga mtima; ndikufuna undibenthulire chinsinsi chako.”

“Chinsinsi?”

Katakwe adasendera chakufupi ndi Kaduya mwakuti pafupifupi nkhope zawo zidaombana. “Bwanawe, muja unkafotokoza kuti udzakhala ndi nyumba, galimoto, ndinkangoona ngati maloto achumba kulota ali ndi mwana; udadziwa bwanji kuti zidzatheka?”

Kaduya adamwetulira. “Sindinkadziwa. Koma ndidali chabe ndi chikhulupiro kuti zidzatheka.”

“Amwene, pano tisakambe mozungulira,” Katakwe adatero akuonetsa kuti sakuugwira mtima. “Ineyo ndikufuna ndimenye mzinga ngati wakowu.”

“Mzinga?”

“Eya. Ndikudziwa kuti pali njomba yomwe udasewera kuti mkulu uja akuninkhe zonsezi.”

Kaduya adagwedeza mutu. “Palibe chomwe ndidachita. Zonse ndi Ambuye.”

“Eyi, osanamizira Ambuye. Zinthu udalandira kuchokera kwa Sofiasi osati Yesu...”

Kaduya adaimirira. “Katakwe, ndimakupilira mzambiri koma sindingalore kuti uzinyoza dzina la Ambuye m’nyumba mwanga muno. *Get out, please.*”

“Amwene...”

“Sindine amwene ako, ndimakusekerera poganiza kuti mwina udzasintha koma ndaona kuti ndiwe wokanika.”

“Aise, ndithandize; wekha ukudziwa momwe nkhufi ndi nsikidzi zimalumira palendi paja-nanenso ndikufuna ndiyambe kufewetsa moyo ngati iwe...”

Kaduya adamudula pokweza manja ake. “Choka mdyerekezi pamaso panga.”

“Mdyerekezi ineyo?” Katakwe adafunsa akudziloza pamtima.

“Munthu aliyense yemwe amanyoza ntchito ya Mulungu ndani?

Mdyerekezi! *Get out!*”

“Aise, sundiululira?”

“*I said get out!*”

Katakwe adaimirira. “Chabwino ndikupita. Koma *let me tell you*

this, I am going to beat you in this game.”

“I said out!”

“You are finished, just watch me,” Katakwe adadukiza namwaza maso
ake mchipindamo “Muli chani muno? I will make money, big money.”

“Out, devil!”

Katakwe adaima pachitseko. “*You know what? You’ve made one terrible mistake.*”

“*What mistake?*” adafunsa Kaduya mopsa mtima.

“Me,” adayankha Katakwe. “Chozizwitsa changa choyamba
ndidzapanga mumpingo wako. *Stupid man!*”

Katakwe adatuluka akulalata.





Mpingo Uyamba

Maonekedwe anyumba yogona alendowo ndi malo omwe idamangidwa adali osagwirizana. Idali yomangidwa mwapamwamba koma dazunguliridwa ndi nyumba zina zosamangidwa bwino mkati wenimweni mwa Chigwirizano. Motero, idali yotchipa kwambiri ndipo ichi ndichifukwa chomwe Katakwe adaisankhira.

Takondwa Jamisoni, bwenzi lake la Katakwe, adakhala mogona pasofa yomwe idali pakona. Zala zake zamanzere zokhala ndi zikhadabo zitalizitali zochita kuikira zidapana ndudu yafodya ndipo mdzanja lake lamanja mudali tambula ya mowa.

Mwana wamkazi adali wokongola mwanjira ina iliyonse. Wofupikira, adali woyerwa ndi wonenepera. Tsitsi lake loikira lalitali lidakuta nkhopo yobulungira ngati dzira nkukagwera mmapewa. Adali ndi maso akuluakulu omwe amayang'ana moleza. Akamasekerera ankaonetsa mano oyera ngati matalala komanso tizidikha tinkakumbika m'masaya.

Omwe amapanga zolochera amai akadayamika kuti namwali amawapititsira bizinesi patsogolo. Nkhope yake idali mbu ndi pawudala yemwe adaphoda, milomo ili psu ndi lipisitiki. Perefyumu yemwe adathira adadzaza mchipindamo ngati achita kufayiramo.

Takondwa adaika tambula ija pakatebulo nkuponya miyendo yake pansi mosalabadira kuti ntchafu zake zidali pamtunda. Adaimilira nakokera bulauzi yake yothina kuti ibise chinkhanira chomwe adajambula pamchombo. Komabe bulauziyo idalephera kukumana ndi siketi yake motero mikanda yomwe adavala mchiuno idali poyerwa.

Mwana wamkazi adadalitsidwa ndi mbuyo ija amati yoswa mtundo ndipo adayenda moyigwedeza nkudzaima pambali pa Likisho yemwe adakhala moyang'anana ndi Katakwe.

“Ngati sukufuna ukhoza kunena,” Takondwa adatero motchalenga, manja ali mchiuno, nganga atadzutsa, mawere atakunga chibakera kufuna kuphulitsa bulauzi. “Tipeza anthu ena oti tigwire nawo ntchito.”

Likisho adapuma mozama. Katakwe amadziwa kuti Takondwa ndi Likisho amapirirana muja amachitira mphaka ndi galu

okhala pakhomo limodzi. Likisho adali mzake waponda apa nane mpondepo pomwe Takondwa adali bwenzi lake. Motero padalibe njira yomwe awiriwa adakazemberana.

Katakwe amadziwa kuti chidani chawo chimachokera pakuti Likisho ankati Takondwa adali wokonda ndalamu moonjeza. Iye amati namwaliyo akaona ndalamu amakha dovu losasiyana ndi galu woti waona fupa.

Likisho ankadandaula kuti msungwanayu ndiye amamuthera Katakwe ndalamu komanso kumulimbikitsa pamaganizo oipa bola kutsogolo kwake kukakhala ndalamu.

“Ine ndimangofuna kuti tione setse kuti tikudziwa chomwe tikuchita chifukwa za Mulungu sizofunika kuchita nazo phada,” Likisho adabwenza mawu, akuyang’ana Katakwe.

“Ndiye zofunika kuchita nazo phada kumene,” Takondwa adatero akuseka monyodola. “Upite mmatchalitchi ukaone masewera omwe anthu akuchita ndi za Mulungu. Utajambula pa kanema anthu akhoza kumatsutsa kuti ukunama ndi zisudzo chabe.”

“Ndikudziwa. Koma tisayambe zinthu zoti tikhoza kuputa nazo minyama,” adalimbikira Likisho.

Takondwa adaseka mpaka kutuluka misozi mmaso. “Utumiki ndi bizinesi yoti anthu akupangira ndalamu osati minyama. Komanso minyama ndi chiyani? Minyama kulibe.”

Diso la Katakwe lidagwa pamzakeyo. Wamfupi ndi wonenepera, Likisho adali mu shati yomwe kolala idayamba kusumbudzuka. Nalo buluku lidawonetsa kuti silikupatsidwa mpata wochoka mthupi. Kuphazi kudali masilipazi.

“Amwene, imeneyi ndi geni yotentha komanso yosafuna kapitolo. Mulungu ndi kapitolo. Anthu ndi makasitomala,” adaunikira Katakwe akumuloza mzakeyo mokweza ndi kutsitsa kuonetsa kuti iye adalibe ndalamu. “Chofunika nkuchenjera pakamwa basi.”

“Ndikudziwa, koma za Mulungu pena pake zimandiopsa,” Likisho adalimbikira. “Mwina Mulungu amachitadi zodabwitsa.”

“Palibenso choopa. Iweyo wakhala ukudyera anthu ovutika, akazi amasiye ndi ena otero, bwanji suopa kuti Mulungu akhoza kukukantha?” adalowererapo mwankhwidzi Takondwa.

“Komanso palibe zoti Mulungu amachita zodabwitsa. Anthu amangogwiritsa ntchito dzina la Mulungu kufuna kudyera anzawo,”

Takondwa adapitirira. “Anthu ambiri akudyera dzina la Yesu, ndani mudamvapo kuti Mulungu wamukantha?”

Likisho adalibe choyankha. Katakwe adatulutsa nyuzipepala. “Uyu ndi Prophet Agujebwe, wa ku Nigeria, ali ndi nyumba za lendi padziko lonse lapansi. Uyu ndi Prophet Zulo, wa ku South Africa, ali ndi bizinesi ya magolosale komanso migodi. Uyu ndi Mbusa Difikoti wa ku Zambia, ali ndi ma esiteti akuluakulu a fodya. A mdziko mwathu muno ndiye ndisachite kuwatchula. Mukudziwa komwe ndalamu zaho zimachokera?”

“Kwa nkhosa zaho,” adayankha Likisho dyera litayamba kuoneka pankhope pake.


“*Exactly.* Monga ndanena ndikufuna ndiyambitse tchalitchi ngati bizinesi ndiye ndikufuna anthu olimba mtima oti akhoza kupusitsa anthu osachitanso mantha kapena chifundo,” adaunikira Katakwe. “Anthu adzidzimuke kuti kwabuka mneneri.”

Katakwe adapitirira. “Utumiki womwe umathamanga komanso suchedwa kukula ndi wamachiritso ndi wazachuma. Motero utumiki wathu umangidwa pangodya ziwiri: ya machiritso komanso chuma.”

Takondwa adazunguza maso ake, nkukweza dzanja lake ngati saliyuti ya msilikali. Adakoka ndudu yake nkumwazira utsi Katakwe ndi Likisho.

“Tsopano tipange *money!*” adatero mwana wamkazi dyera likuwala pankhope pake mosasiyana ndi mphaka woti wagwira khoswe.





Chozizwitsa Choyamba

Mbusa John Kaduya adaonetsa kuti sanamusungire Katakwe ngawa ina iliyonse. Adamulandira Katakwe patchalitchi pakepo mwaulemu ndi mwachisangalalo. Tchalitchiyo idali mkati momanga, makoma ndi denga lokha ndizimene zidali zitatha.

Katakwe adafika ndi Takondwa ngati anthu otchuka a mmakanema m'galimoto ya hayala yapamwamba yaphuliphuli moperekezedwa ndi akulu ampingo atatu omwenso nawo adafika mmagalimoto ovuta. Takondwa adanyamula katoni mmanja.

Nyumba ya Mulunguyo idali yodzaza theka lokha. Katakwe adakumbukira kuti nthawi yomwe adasuzumiramo koyamba miyezi ingapo yapitayo anthu adali odzaza mosowa pokhala. Adadziwiratu chomwe chimasefa anthu mumpingomo—Kaduya sankaumira kudzudzula nkhosa.

“Monga tidalengezera sabata yatha, yemwe atigawire uthenga ndi Prophet Katakwe founder wa *Miracles and More Miracles Ministries*,” Kaduya adalengeza.

Katakwe adapita kutsogolo akunjanja ngati katswiri wankhonya akamalowa mbwalo. Kuguwako adangofikira kuimba kwinaku akujowa.

“Yesu moto!” iye adatsogolera akukweza manja kuonetsa kuti mpingo uyime.

“Moto!” udayankha mpingo ukuimirira.

“Nanga satana?”

“Aaaa utsi ubo!”

Adatsika kugomeko nkuyamba kuthamanga. Adayamba ndi akulu ampingo adabwera nawo aja kumulondola pambuyo kenaka mpingo wonse udalowerera ndipo posakhalitsa mpingo wonsewo udapezeka ukulondola pambuyo ngati akusewera follow the leader kwinaku nyimbo ikupitirira kuti Yesu moto, moto, nanga satana, aah butsi ubo!

Mwadzidzidzi Katakwe adabwereranso kuguwa. “Mumpingo muno mukuoneka kuti muli chiwanda cha umphawi. Panjapa ndangoonapo timagalimoto tingapo. Koma lero wodzozedwa wa Yehova ali pamaso panu; zonse zisintha!”

Nthungululu, kululutira ndi malikhweru adadzaza tchalitchiyo.

“Umphawi sigawo la ana a Mulungu. Yesu atafunsidwa kuperekwa msonkho adauza Petro akawedze nsomba. Ataikanula adapezamo ndalama.

Wosakhulupilira angakhulupilire kuti zimenezi zikhoza kutheka?”

“Ayi!” mpingo udanyakha.

“Yesu amaika ndalama pena paliponse; ndalama zimenezo timazitcha *miracle money*,” Katakwe adaptirira. “Lero sindilalika; ndingowonetsa mphamvu yomwe Yesu amachita pa ana ake kuti apeze ndalama. Mai busa, ndipatseni katoniyo.”

Takondwa adapita kuguwa akugwedeza thupi ngati ali pa *fashion show*, nsapato yachidende chachitali ikugogoda pansi. Suti yake yofiyira yonyezimira idali yogwira thupi ndipo idawonetsa ndendende momwe thupi lake lidaumbidwira.

Katakwe adatenga katoni ija nkulunjika komwe kudakhala anthu n’kumagawa ma yunivolopu. Adagawa kwa anthu khumi.

“Aliyense ayang’ane muli chiyani muyunivolopu yomwe walandira,” iye adalamula.

Onse adayang’ana mkat. Adatsimikiza kuti mudalibe kanthu.

“Ndipatseni mayunivolopu amenewa ndipo Mulungu aikamo chosowa chanu,” adalosera Katakwe.

Mayunivolopu aja adawaponyanso mukatoni muja. Adayamba kupemphera mmalirime. Kenaka adawauza anthu aja kuti aliyense adzatengenso yunivolopu yake ndipo ayang’ane mkat muli chani.

Woyamba kutola adali gogo wina, adapeza kuti muli sate sauzande. Mai wina adapeza fifite sauzande. Anthuwo adapezamo ndalama zosiyanasiyana.

Bambo wina mpaka adapeza handede sauzande.

Anthu onse mtchalitchimo adaonetsa kuti azizwa. Ngakhale mbusa Kaduya amene adangoti maso tong’ole, kukamwa kuli yasa.

“Zimenezi ndiye timati miracle money...ndalama za zatheka bwanji!” adakuwa Katakwe. “Ndiye mwakonzeka kulandira mdalitso wanu?”

Momwe umatha mwambo wamapemphero, Katakwe adaona ulema mmaso mwa mbusa Kaduya.

“Munthu wa Mulungu, Ambuye wakudalitsanidi,” iye adatsimikiza akumuperekeza Katakwe ku galimoto. “Pamoyo wanga sindinaonepo zozizwitsa ngati mwachita zija.”

Katakwe adayang’ana kumwamba. “Monga mwakhala mukunena, *man of God*, ndi Mulungu wathu palibe cholephereka.”

“Ameni,” Kaduya adavomereza.

Maso a Katakwe ndi Takondwa adaombana. Iwo adaona kuti mbusayo amakhulupirira kuti pachitikadi zodabwitsa. Maganizo awo adali ofanana; ngati adatha kumupusitsa mbusa poyerayera, nanga bwanji anthu ena?

Chifukwatu Katakwe sadachite chozizwa chilichonse. Katoni ija idali yodula pakati. Mbali ina adaikamo mayunivolopu opanda kanthu pomwe mbali ina adaikiratu mayunivolopu okhala ndi ndalamama.

Chomwe adachita chidali choti adangotembenuza katoni ija nkupereka ma yunivolopu adaikiratu ndalamama aja. Mwachidule, anthu aja adawadyetsa njomba chabe ngati muja amachitira anthu a wachiona ndani!





Njoka Yokalamba

Msonkhano wachitsitsimutsowo udalengezedwa bwino ndipo anthu adafika mwaunyinji wawo. Kwa miyezi itatu, Likisho ndi Takondwa adakhala akufalitsa mbiri yazozizwitsa zomwe ankati Katakwe akuchita.

Zonse zidali zabodza koma amati kalowa mkhutu kayanza komanso mbuto ya kalulu idakula ntadzaonani; mbiri yamphamvu zomwe Mulungu adaikiza mwa Katakwe idapita patali. Anthu amachoka kutali kudzakumana naye kuti adzawapempherere.

Motero atalengeza kuti ali ndi msonkhano wachitsitsimutso, anthu adakhamukira kumeneko kuchokera ku ngodya zonse zadziko la Malawi.

Aliyense adafuna kukadzionera yekha mneneri yemwe Mulungu adadzutsa.

Munthu wapentekosite akati wadalitsika, amanena kutengera ndi chuma chomwe wapeza. Motero, munthu wapentekosite sangati ndiwodalitsika pomwe umphawi sukumuchoka. Pachifukwa chomwechi, ngakhale abusa amene, amayesetsa kupata chuma chochuluka ngati umboni wakuti Mulungu akuwayendera mwapadera.

Zidakakhala zosamveka Katakwe kumatindi munthu wodzozedwa wa Yehova umphawi utamukakamira ngati litsiro lamwana woweta ng'ombe.

Motero, iye adatulukira pamsonkhanowo pamdipiti wamagalimoto omwe adapanga hayala. Adatsika limodzi ndi mabodegadi awiri omwe adali mumasuti ndi magalasi akuda. Achitetezo awiriwa adapanga njira mkhamu la anthu adasonkhanawo kuti Katakwe adutse mopanda vuto.

Katakwe adali atatchena movuta. Adali msuti yonezemira yomwe idali phuliphuli m'dzuwa la masanawo. Kumutu adavala wigi yakuda yomwe imangooneka ngati tsitsi. Nsapato yomwe adavala idali ya nyezinyezi ngati suti yakeyo.

“Wokondeka, ndidatha masiku khumi opanda chakudya kapena madzi paphiri la Dedza. Ndipo pamenepo, ndili pakati pa imfa ndi moyo kaamba kanjala, Mulungu adandionekera. Iye adandiuzza kuti Katakwe, ana wanga, ndidakudzoza ngati mpulofeti usadabadwe.

Ndakuzula mmachimo momwe udamira ngati nkhumba ndipo ndakuyeretsa. Tsopano ndikukutumiza kuti ukaphwasule maukulu ndi maumfumu,” iye adatero atakwera pansanja akulankhula kudzera mu chimkuzamawu.

“Kwa omwe simukudziwa, mpingo wathu uli pa JJ Primary School.

Muzibwera kuti mudzalandire chosowa chanu. Odwala akuchira, osaona akuona, osayenda akuyenda, mizimu yoipa tikuiswa,” iye adakuwa akuponya chibakera ngati akuphwanya mizimu yoipayo. “Tidzatsegula mfungulo wa mdalitso wanu-mudzapeza ntchito, kukwezedwa pantchito, kupeza mabizinesi, kupeza mabanja, kuchizidwa matenda.”

Adadukiza napemphera kwa kanthawi mmalirime. “Pamsonkhano pano tiwonetsa mphamvu zomwe Mulungu wandipatsa. Tsopano muona ndi maso anu mphamvu yomwe Mulungu waika mwa ine, wodzozedwa wake.

Omwe mufune kuima nane, mutsalire tikumane ukatha msonkhano. Pano ndikufuna kuonetsa zomwe Mulungu amachita.”

Iye adadukiza ndikuyang’ana kumwamba. “Likhathara likhethere! Pano ndikuona dzina ili muuzimu...aaa M...A...R...I...” adadukiza napsinya maso ake muja amachitira munthu wosaona bwino akamayang’ana chinthu choti chili patali. “Akuoneka ngati H...No. ndi...A. MA-RI-A... Maria.”

Adayendayenda monyada pansanjapo. Adaima nayang’ananso kumwamba kuja. “Likhathara, likhothore...toni nambala yake ndi...” adadukiza kenaka nkuitchula “ndipo amakhala ku Kawale. Wavala dilesi lachikasu. Maria afike kutsogolo kuno. Akachedwa nditchula ngakhale mtundu wa panti yemwe wavala!”

Msungwana wovala dilesi lowala lachikasu adavumbuluka mgulu la anthuwo nathamangira kutsogolo kwinaku akukuwa, “*I will destroy you, man of God!*”

Kutsogoloko msungwanayo adangofikira kuponya zibakera zomwe Katakwe adazizinda. Achitetezo adafuna kumugwira koma Katakwe adawaletsa. Mmalo mwake adatulutsa botolo la madzi oyera n’kuyamba kumuwaza msungwana uja.

“Lisondoro likhatchala! *Fire on your body!*” Katakwe adakuwa. Msungwanayo adayamba kundengula kwinaku akukuwa ndi kudzigwiragwira ngati ali pamoto. “*Leave me alone, man of God!*” “*Who are you?*” adafunsa Katakwe.

“Ndine njoka yokalamba yochokera pansi panyanja,” adayankha msungwanayo akuoneka kuti ali paululu woopsa.

Katakwe adamuthiranso madzi oyera aja. “*What is your mission here?*”

“*To destroy you and your ministry, holy man,*” adayankha msungwanayo.

“Libosaya; *the devil is a liar!* Nthawi yako yatha, demoni,” adakuwa

Katakwe. “*Out of her body! Out!*”

Msungwanayo adagwa pansi nayamba kudzigwedeza ngati akutsalima.

Katakwe adapitirira kumupempherera mpaka izi zidasiya. Adamuuza kuti aimirire.

Msungwanayo adaimirira, tsopano akuoneka kuti mtima wakhala pansi.

“*Sister, do you know me?*” msungwanayo adakana. “*Have we met before?*” adakananso msungwanayo. “*So how did I know you?*”

“*I don't know, man of God,*” adayankha msungwanayo.

Katakwe adagwedeza mapewa. “*Likhothala!* Chifukwa chiyani umafuna kundiwononga?”

Msungwanayo adafotokoza kuti ndi wa sataniki. Iye adati kumidima kudagwedeze ka ndi kudzuka kwa mtumiki Katakwe. Motero atakumana pansi panyanja adatumizidwa kuti adzaononge utumikiwo.

“Motani?”

“Mabodza, ineyo ndidakayamba kufalitsa mbiri yoipa yabodza ya inuyo pulofeti-kuti ndinu wasataniki, mumasanduka njoka, mphamvu zanu mumazitenga kumidima-china chili chonse choti anthu asakukhulupirireni.”

“*Hikhopholotha; the devil is liar!*” Katakwe adakuwa.

“Ndikulengeza kuti kuyambira lero ndiwe mwana wa Yesu ndipo

ukhala ukutumikira nane limodzi. Utumiki weniweni umagwedeza kumidima. M'manja mwa Yesu."

Katakwe adadukiza napemphera mmalirime atapatsa gulu lonse msana wake. Kenaka adatembenuka mwadzidzidzi. "Pano ndikuona bambo wina wavala malaya akhakhi ndi buluku lakuda. Bamboyu wakhala akuyendera ndodo moyo wake wonse. Dzuka pamenepo lero nditsiku lomwe Yesu akuyendere."

Mkulu wina adaima pomwe adakhala ndipo adayenda movutikira kupita kutsogolo. Adali chithunzithunzi chomvetsa chisoni, mbali yonse yakumanzere idali yopuwala kuyambira kumutu mpaka kumiyyendodiso lopsinya, mlomo wopotoka, khosi litapindika, dzanja lili lopuwala, mwendo akuwuguguza. Adadziguza akutsamira ndodo yomwe adaigwira ndi dzanja lamanja.

"Lero uyenda mdzina la Yesu!" Katakwe adakuwa nayamba kupemphera mmalirime. "*Libobobobo libababababa...*" Atapemphera kwa kanyengo, mkuluyo adayamba kunjenjemera ngati munthu wamanjenje. Kenaka diso lidatseguka, mlomo kuongoka. Pang'onopang'ono dzanja ndi mwendo zidayamba kuongoka mpaka zonse zidalunga.

"Lisathalaka! Onetsa dziko lapansi zomwe Ambuye akuchitira," Katakwe adatero. "*Shame the devil!*"

Poyamba mkuluyo adayenda mwapendapenda ngati mwana wophunzira kuyenda. Kenaka adayamba kuthamanga, kujowa ndi kuvina akukuwa kuti Ambuye ndiwabwino.

"Palibe chomwe ndingathe kubwezera kwa Mulungu kuposa kujoina utumiki wa munthu wa Mulunguyu kuti ndikhale chitsanzo cha mphamvu za machiritso zomwe Mulungu waika mwa wodzozedwa wakeyu," adalengeza mkuluyo.

China chomwe chidadabwitsa anthu kwambiri patsikulo ndi machiritso a bambo wina wake wamisala. Munthuyo, yemwe adavala chibulandi chokutha, ankaoneka kuti adali wachiwawa chifukwa adali atatumanga ndi zingwe zakhonje ndipo ankavuta muja amachitira galu wovuta ukamapita naye kudibi. Anthu awiri adamuperekeza kutsogolo kuti akapemphereredwe.

Atangofika kutsogoloko, munthu wamisalayo adadula zingwe zija.

Adachitsakamula chibakera ndipo mmodzi mwa omwe adamuperekeza aja adagwa pansi osadzukanso. Wachiwiri uja adalandira theche lammimba ndipo adagwa pansi akugubuduka ndi ululu.

Katakwe adatulutsa madzi ake oyera mwachangu namuwaza wozungulira mutuyo. Wamisalayo, yemwe ankati aziponya chibakera, adabwerera mmbuyo akudzikanda ngati wawazidwa chitedze. Katakwe adapitirira kumuwaza munthuyu madziwo kwinaku akupemphera mmalirime.

Bamboyo adayamba kusanza pomwe amapemphereredwa. Adasanza zinthu monga malezala, mipeni ndi zithumwa.

Gulu la anthulo lidagwidwa ndi mantha komanso ulemu. Nthawi yonseyi nkuti a makamera akujambula ndipo zodabwitsazi zikuoneka mmakomo a onse omwe ankaonera channel ya television yomwe inkaonetsa zithunzizo.

Pa TVpo adaonetsa mai wina yemwe adaonetsa kuti wagwidwa mtima ndi zochitikazo. Adali mai woyeru ndi wooneka waulemu wake. Adali Anna Yakobo, mai wodziwika bwino pa nkhani ya bizinesi. Iyeyu adali mwini wake wa kampani ya Nagama Investments yomwe inkakumba zitsime.

Maiyu adanena mawu, ndipo mawuwo adaphera mphongo maganizo a ambiri omwe adafika pamsonkhanopo.

“Zoonadi, munthuyu ndi wodzozedwa wa Yehova,” adadzilankhulira mai Yakobo.

Ngati kuti adamva mawu akewo, maiyo anadabwa maso a Katakwe atagwa pa iyeyo.

“Mulungu wandinong’oneza kuti pano pali mai wina yemwe wakhala akuvutika ndi matenda osachiritsika,” Katakwe adafuwula. “Lero mayi ameneyu achira.”

Pamsonkhanopo padati zii, chiyembekozo chikukwera mwa amai ambiri omwe adali pamalopo.

“Mulungu akundiuzza kuti maiyu ali kampani yake,” adadukiza nayang’ana mmwamba. “Dzina la kampaniyo ndi Na...Na...Ga...
28

Ma...Nagama Investments. Mwini wake wa Nagama Investments afike kutsogolo kuno.”

Anna Yakobo adali chithunzithunzi chodabwa. Adadzuka pomwe adalipo atazungulira mutu ndi chimwemwe.

“*Here I am Holy Man,*” adakuwa mai Yakobo akuthamangira kunsanja.

“Mai, mukudwala matenda osachirtsika,” Katakwe adaulula.


“Yes, man of God. I am HIV positive,” adavomera mai Yakobo. “Makalata akuchipatala ndi awa. Mankhwala omwe ndimamwa ndi awa.”

Katakwe adatenga mapepala aja nkung’ambang’amba. Adakwatula ma ARV aja kwa maiyo nkuwakhuthulira pansi nkuwapondaponda.

“Libabakhatha masondoro,” Katakwe adapemphera. “My daughter, you are healed,” iye adalengeza. “Mankhwala osadzamwanso.”

Mayi Yakobo adjowa ndi chisangalalo. “I am healed. Thank you Jesus!”

Pamsonkhanopo padalowa chipwirikiti pomwe gulu la anthu lidakhamukira kutsogolo kuti akalipempherere.





Mpingo Ukula

Anthu ambiri adatsalira kuti awonane ndi Katakwe. Anthuwa adakakumana naye ku hotela yomwe amagona nthawi imeneyo. Aliyense amakumana ndi Katakwe payekhapayekha. Mmodzi mwa anthuwo adali mai Yakobo.

Komatu kuonana ndi Katakwe sikudali ulele. Munthu amayenera kupereka ndalamu yochuluka.

“Dadi, ineyo ndidabadwa mwatsopano ndidakali buthu koma pamoyo wanga sindinaonepo zodabwitsa ngati zomwe mwapanga lero pamsonkhano paja,” mai Yakobo adatsimikizira.

Chamkati Katakwe adamwetulira. Zaka zake zobadwa zidakatha kulowa kawiri mwa zamaiyo koma amamutchula dadi-bambo. Ena ankamutchula papa. Ena baba. Maina a ulemu.

“Libosaya mandrere, ine ndine chotengeramo chabe cha Ambuye.” Katakwe adadzichepetsa.

“Papa, ine ndikufuna ndiyime nanu mu utumiki wanu,” adafotokoza maiyo.

Katakwe adafuna kuvina ndichikondwerero. Panopa adali mngongole zoopsa zomwe adakwereta monga mpamba woyambitsira utumiki wake. “Ukufuna kuima nane motani, mwana wanga?”

“Malemu mwamuna wanga adandisiyira bizinesi yokumba mijigo. Pakatipa bizinesiyo siyimayenda bwino malinga ndikuti ndimadwaladwala koma muja mwandipempherera ndikumva bwino kwambiri ndipo ndikudziwa zinthu ziyamba kuyenda bwino. Koma panopa pokuthokozani ndizikulipirirani kaye lendi yanyumba yanu.”

“*Halala lisokhala; Praise the Lord!*” adakuwa Katakwe.

“Koma Ambuye akangondipatsa kontrakiti ina yake, Man of God ndikuchitirani zodabwitsa,” adalonjeza munthu wamaiyo.

Mtima wa Katakwe udadumphu mothamanga ndi chikondwerero. Zipatso za bizinesi yake zidayamba kupsa tsopano. “*The devil is a liar.* Mai, fotokozani chokhumba chanu ndipo monga mwalandirira machiritso, Mulungu akupatsaninso kontrakiti mukufunayo. Lero ndi tsiku lanu.”

“*Man of God,* pali kontrakiti ina yomwe ndimaifuna kwambiri.

Koma yakhala ikulephereka,” maiyo adatero ndipo adafotokoza zonse zokhudzana ndi kontrakitiyo.

“*Libosaya; the devil is a liar,*” Katakwe adabwerezza. “Ndi Mulungu wanga palibe cholephereka.”

Iye adayamba kupemphera. Komatu kupempheraku kudali kunja chabe, mkaati adali akudya mutu. Kontrakiti amanena maiyo idali ya mamamiliyoni ambiri. Uwu udali mwai wake woti alowetsepo dzanja lake pa kontrakitiyo.

“Mwana wanga, dikira pompano ndikalankhule kaye ndi Ambuye.”

Iye adapita kukadzitsekera mchipinda chomwe amagona nkuyamba kupemphera mmalirime mokuwa. Patatha mphindi zisanu adatulukira.

“Mwana wanga, ndalankhula ndi Mulungu ndipo wandiululira kuti ndi satana mdyerekezi yemwe akulepheretsa kontrakitiyi ndi cholinga choti ntchito ya Ambuye isapite patsogolo. Koma Mulungu wandifotokozena kuti kontrakiti upatsidwa koma poyamba upange chowinda.”

“Chowinda?”

“*Likhetele,*” Katakwe adavomera akudzigwedeza ngati nkhuku ikamakutumula madzi kunthenga. “Chowinda, mwana wanga. Kuyambira nyengo zakale, Ambuye amaputidwa kupanga kanthu kudzera mma puleji. Gideon, Hannah ndi ena otero adapanga zowinda ndipo zofuna zawo zidaperekedwa.”

“Baba, ngati Mulungu angandipatse kontrakiti imeneyi, ndidzamupatsa zonse zomwe ndili nazo panopa.”

Katakwe adamuyang’ana. “*Likhathakha; zitchuleni.*”

“Galimoto yomwe ndikuyendera panopa ndi nyumba yanga ku Area 43,” adalonjeza mai Yakobo. “Chifukwa ndikangopata kontrakiti imeneyi ndikhoza kugula magalimoto ngati amenewa makumi awiri ndikumanga nyumba khumi zoposa imene ndawindayi.”

Katakwe sadakhulupirire mwai wake. Tsopano adapeza danga lopeza galimoto ndi nyumba. Adalakalaka John Kaduya adakakhala po aone zomwe ankatanthauza tsiku lijali.

Koma kwa maiyo adati: “Mwana wanga, wapanga chowindamu wakwaniritsa chokhumba cha Mulungu. Ndipo monga umfumu udalandidwa kwa Belisazara nkuperekedwa kwa Dariyo Mmedi, kontrakiti imeneyi lero yalandidwa kwa yemwe adaiwina ndipo yapatsidwa kwa iwe. Mwezi wamawa udzachitira umboni wa izi kuchihema cha Ambuye.”

Indedi, mwezi wotsatira mai Yakobo adadzachitira umboni monga adalosera Katakwe.

“Mpingo, sindikudziwa kuti ndiyambire pati koma munthu wa Mulungu akamanena kuti tipereke kuti tidalitsike, tiyeni tisamayese akungocheza.

Padali kontrakiti ina yake imene ndinkaifuna kwambiri. Adandiua kuti sangandipatse chifukwa kampani yanga idalibe zoyenereza.”

Vuto limene limakhala ndi anthu opemphera nchiyani? Katakwe adadzifunsa. Okha amadziwa kuti chinthu sicingatheke koma amayembekezera kuti Mulungu awapangirebe chifukwa apempha. Kodi kumeneku sikukhala kufuna kupeza chinthu chomwe sanayenera kulandira? Koma mokuwa adati, “Fotokozani, *sister* zomwe Mulungu wakuchitirani!”

Mai Yakobo adapitirira. “Ndidakapempha a pulofeti kuti andipempherere. Ndipo ndidawinda kwa Mulungu galimoto ndi nyumba yanga akadzandipatsa kontrakitiyo.”

Katakwe adaluma mlomo wammunsi. Mai Yakobo amati kampani yawo imene siyidali ndizoyenerera ipambana bwanji kontrakiti? Ngati Mulungu angapangitse kampani yolephera kuwina sindiye kuti naye ndiwachinyengo? Pamaso adakuwa, “Tiuzeni zomwe Ambuye akuchitirani!”

“Ambuye andininkha kontrakiti ndipo ndaima pano kudzakwaniritsa chowinda changa kwa Yehova. Munthu wa Mulungu, nawa makiyi a imene idali nyumba ndi galimoto yanga. Nawanso mapepala, zonse ndasinthia kale mudzina lanu.”

Akuyenda kukalandira mphatsozo, Katakwe adapitirira kudya mutu. Mai Yakobo adali munthu wozindikira bwino. Njira yoperekera ma kontrakiti amaidziwa. Maiwo amaganiza

kuti Mulungu adachita chiyani kuti mpaka asinthe zotsatira za maperekedwe a kontrakiti?

Adamwetulira atakumbukira kuti amai ena amakhulupirira kuti mpaka Mulungu akhoza kusintha kuti mwana woti anali wamkazi akabadwe wamwamuna. Ngati Mulungu amafuna izi zichitike sadakangopangitsa mwanayo akhaliretu wamphongo mmalo movutika kudzasintha kutsogolo? Ngakhale atati asinthe, phindu lake lingakhale chiyani?

Ichi nchifukwa pamafunika anthu otere kumawakhaulitsa mopanda chifundo, Katakwe adadzitsimikizira. Iye adakumbukira zomwe adachita kuti kontrakiti itheke.

Iye adapeza kuti mkulu wa kampani ya Saracen Industries adali ndi chibwenzi pabala ina yake. Adapangana ndi msungwana yemwe adali pachibwenzi ndi mkuluyo kuti akawatole zithunzi zosayenera. Msungwanayo adavomera atamulonjeza ndalama zambiri ndipo zithunzizo adajambuladi.


Katakwe adadzizimbaitsa ngati munthu wina ndipo adakumana ndi mkuluyo. Adamuuza kuti apereke kontrakiti kwa mai Yakobo kupanda kutero atumiza zithunzinzo kwa mkazi wake komanso kuziyika pa intaneti.

“Ndikaziyika pa intaneti ndiye kuti ntchito yanu yatha,” Katakwe adamuopseza mkuluyo. “Tidzakamba nkhaniyi ndi yemwe adzalowe mmalo mwanu.”

Mkuluyo sadakachitira mwina koma kupereka kontrakiti yomwe mai Yakobo amanena monyadira kuti Mulungu wawapatsa.

Katakwe adalandira makiyi ndi mapepalawo monyadira. “Mpingo, ngati Mulungu akhoza kuchita izi kwa Mai Yakobo, angalephere bwanji kuchita kwa inu? Motero ndikulengeza kuti sabata ino ndi sabata yobyala. *Now let's shame the devil; bring your seed and the Lord shall grant you all your wishes!*”

Tchalitchi idayaka moto. Akhristu adalemba macheke, ena adapereka ndalama, ena adawinda.





Mphwanu ndi Big

Katakwe adakalowa mnyumba adamupatsa mai Yakobo ija. Idali nyumba yokongola yolkhala mumpanda. Ankayenderanso galimoto yapamwamba ija adawinda maiyo.

Patangodutsa miyezi khumi chichitire msonkhano uja, malume ake a Topitopi adatulukira tsiku lina lake mwadzidzidzi. Udali mmawa, dzuwa litangothamangitsa kumene mame.

Sadali atali kapena afupi, onenepa kapena woonda. Tsitsi lawo ankalisitabe ndi mwala wamoto mu sitayilo ya matchona a mma 1980. Monga mwa nthawi zonse, iwo adali mu imodzi mwa masuti awo omwe adachoka nawo ku Jubeki. Ngakhale sutiyo idali yotuwa, koma idali yochapidwa ndi kusitidwa bwino. Kuphazi adavala nsapato yakuda yosongoka.

“Ankolo!” Katakwe adawalandira modabwa. “Nkwabwino kulawirira kotere?”

“Hawu! Nyumba ino ndiyako?” adafunsa a Topitopi.

“Yanga, malume,” adavomereza Katakwe. “Tiyeni tilowe mnyumba.”

Katakwe adaona malume akewo akumwaza maso mnyumbamo. Sofa yomwe adakhala idali yapamwamba, matebulo adali agalasi ndipo mudali chikanema chachikulu kwambiri. Chilichonse mchipindamo chidali chapamwamba.

“Hai, mphwanga, ndiulule. Ndoramva kuti udayamba utumiki sindimakhulupirira. Ndimangoti ndizomwe zoonjezera za anthuzi. Ndiye dzulo ndinaonera msonkhano wako woyamba womwe unabwerezedwa pa kanema. Sindinakhulupirire nditaona zodabwitsa zomwe umapanga,” a Topitopi adafotokoza. “Mfowethu, Ambuye akudalitsadi.”

Katakwe adaseka. “Malume, pamene paja padalibenso chozizwitsa chomwe chimachitika.”

Nsidze zamalumewo zidalukana. “Ukutanthauza chiyani?”

“Tsibweni, utumiki ndidayambawu ndi bizinesi,” Katakwe adawatsina khutu mmaso muli gwa.

“Chani?”

“Sindinaitanidwe kapena chani, malume; ineyo ndidangowona kuti utumiki ndi bizinesi yotentha,” adabwerezza Katakwe.

Malumewo adayendetsa dzanja mmutu. “Sindikumvetsa.”

“Ankolo, lingaliro lotsegula bizinesiyi lidayamba nditaona zomwe zidamuchitikira mnyamata uja ankapanga utumiki nthawi ija ndinkakhala ku Chinsapo,” adayamba nkutero Katakwe.

“John Kaduya?” adafunsa a Topitopi.

“Mwalasa, tsibweni. Iye uja adapempherera mkulu wina. Mkuluyo atalemera, adadza kudzathokoza pomugulira nyumba ku 47 ndi galimoto ya mtundu wa Mercedes Benz.”

“*Aikona! Ukhuluma truth?*”

“Ndithu, malume,” adatsimikiza Katakwe. “Motero nane sindinazengereze, ndidakakwera phiri, kukamwera mavesi, basi potsika pamenepo nkuwauza anthu Mulungu wandiyitana. Ndiyetu utumikiwu.”

A Topitopi adatulutsa kabotolo kaphanthi ka kachasu. Katakwe adawalanda mwachangu nalowa kuchipinda. Adatuluka kumeneko ndi mkunda wa *brandy*.

“Malume, mphwanu tsopano ndi *big*,” Katakwe adanyadira akuwathirira malumewo mowawo mu tambula yagalasi. “Panopa muyamba kudyerera.”

Malumewo adazukuta botololo modabwa. Katakwe adayankha funso amalephera kufunsa tsibweni akewo. “Paja ndanena kale kuti utumikiwu ngwa feki. Beer ndimapsipsinthabe koma mobisa.”

“*Aikona, chomwe sindikumvetsa ndipo ndichomwe chandifikitsa pano chinali chakuti ndinadzionera ndekha pakanema ukuchita zozizwitsa,*” adafulula malumewo. “Ndimafuna ndidzamvetsetse kuti zimatheka bwanji?”

Katakwe adaseka kwinako akupukusa mutu. “Malume, ndakuwuzani kale kuti palibe chozizwa chimachitika pamene paja. Zija ndimapanga zija zonse ndizabodza. Nditiati ndifotokoze nokha muona kuti nzosavuta”

Malumewo adapopa mowa onse uja, nkupuma momva bwino. Adaiperekatambula ija kwa Katakwe yemwe adatsanuliramo mowa winanso. “Tafotokoza.”

Naye Katakwe adatenga tambula ina yomwe adathiramo *brandy* yemwe adaphatikiza ndi Cocacola. “Msungwana uja ankati

ndiwakumidima uja ndi Yaliyali, hule lomwe ndimacheza nalo kwambiri ku Kawale. Ndidiamuwuza kuti akapange zimene zija ndipo ndidamulipira.”

Kukamwa kwa a Topitopi kudati pululu.

“Zonse zimapangidwa pamene paja zidali zopangana. Mkulu uja ankanamizira kuti ndiwopuwala uja ndi Joe Gada. Iye uja ndiwalungalunga koma amatha kudzipangitsa kuti azioneka ngati wolumala akamapempha ku Limbe. Imene ija idali acting.”

Nkhope ya a Topitopi imangowoneka ngati ya munthu woti akumva mawu a munthu wakufa.

Katakwe adaptirira. “Uja ankanamizira kuti ndiwamisala uja ndichidakwa chinachake cha pa Kamwendo. Ndidiangomuuza kuti azikanamizira kuti ndiwopenga. Zija ankakhala ngati akusanza zija ankatulutsa mchibulandi adavala chija. Malipiro ake ndidamugulira mikunda ingapo yakachasu.”

“Nix, sungakhale kuti onse aja udapangana nawo,” a Topitopi adaonetsa kuti sadamvetsebe.

“Ena ndimakhala kuti ndafufuziratu mavuto awo. Monga mai aja ndinkati ali ndi HIV, ndidali nditamva kuchokera kwa Likisho,” adaulula Katakwe.

“Nanga poti udawaletsa mankhwala?”

Katakwe sadayankhe. Mmalo mwake adati, “Pali njira zina ziwiri zomwe ndimagwiritsanso ntchito. Ena amati akafika amafotokoza kwa olandira alendo mavuto awo ndiye olandira alendowo amanditsina khutu; ine nkatero ndimakhala ngati Ambuye andiuza. Zina ndimangonenapo. Mwachitsanzo, ndimadziwa kuti pagulu la anthu ambiri sipangalephere kukhala wina woti akudwala, banja silikuyenda bwino kapena ali ndi mavuto ena otero. Ndiaktero ndimawapempherera. Ndimadziwa kuti chomwe amafunacho chikachitika basi azidzati ndine.”

A Topitopi adapuma mozama nazunguza mutu wawo wopanda nyanga. “Hayi, koma suchita mantha kuti Mulungu akhoza kukukantha?”

Katakwe adagubula mowa uja. “Pali atumiki ambiri omwe akuchita chinyengochi, bwanji Mulungu sakuwakantha?”

“Chuluke chuluke ngwanjuchi; ine ndikufunsa za iwe,” adasongola a Topitopi.


Katakwe adeseka. “Ankolo, mautumiki amasiku ano ndi mabizinesi. Mulungu ndi kapitolo ndipo nkhosa makasitomala.”

“*Ukhuluma so, umshana?*”

“Malume, pali chinthu chomwe anthu akupindula ndi mautumiki abodza ngati athuwa,” Katakwe adadziteteza. “Mawa tipitire limodzi kutchalitchi mudzaona chomwe ndikutanthauza.”

A Topitopi adagugudiza mowa onse uja. “*Hei, wena, hamba kwa hell;* ndikubwerera. Ine sindikufuna kuputa dala mkwiyo wa Yehova. Komanso dziwa ichi-utumiki wabodza sukutha mtunda.”

Katakwe adaseka chikhakhali. “Nanga wangawu ukapita patali?”





Mayendetsedwe a Mpingo

Mpingo wa Katakwe udali muholo yasukulu ina yake yapulayiveti. Pomwe mkaati mwa sabata imagwiritsidwa ntchito zina ndi eni ake a sukuluyo, tsiku la sabata inkasanduka kachisi. Patsikuli, kutsogolo kwa holoyo kumakongoletsedwa ndi nsalu zokongola ndipo guwa lapamwamba lagalasi limaikidwa.

Mmodzi mwa akhiristu adali atagula zida zoimbira zomwe zimagwiritsidwa ntchito ndi a gulu la Matamando lomwe limangodziwika ndi dzina la chingerezi loti *Praise Team*. Gululi limakhala kutsogolo.

Pofuna kuteteza udindo wake, malonje a mpingowo adali akuti kutsutsana ndi mbusa ndikutsutsana ndi Mulungu kutanthauza kuti kutsutsana ndi Katakwe kudali chimodzimodzi kutsutsana ndi Yehova. Motero padalibe yemwe ankatsutsa zonena za Katakwe. Dzina lake lodyera la utumiki lidali *Miracle Maker*—mpangi wazozizwitsa.

Mpingo wonse umakhala moyang'ana kutsogoloko. Laini yoyamba idali ya Katakwe ndi akulu ampingo. Ngakhale sadamange ukwati, Takondwa tsopano adali mai busa ndipo amakhala nawo kutsogoloko limodzi ndi Katakwe. Kuchokera apo, munthu amayandikira kutsogolo kutengera ndi kufunika kwake. Ngati ndiwe mlendo, olandira alendo, omwenso amangodziwika ndi dzina lachingerezi lakuti ma *usher*, amakuyang'ana momwe ukuonekera. Ukakhala kafansianji, amakusiya kumbuyo, ukakhala wooneka kuti ndalamu sizikutalikira amakakukhazika kufupi ndi kutsogolo.

Mwambo wamapemphero umayamba mmawa ndi mapemphero omwe amawatcha *intercession*—amapemphera kaye kuphwanya magoli ndi mphamu za satana pampingopo. Kenaka amalowa mgawo la matamando, lomwe kumakhala kuvina sitayilo ina iliyonse yomwe munthu angafune. Iyi imakhala ngati njira yotakasira Akhristu.

Akhrisitu atayaka ndi kuvinako, pamakhala uthenga wachopereka womwe cholinga chake kumakhala kulimbikitsa mpingo kuti upereke. Mpingo kenaka umapereka ukuvina ngati pachikwati. Akatha kupereka, amavinanso kukondwerera ndipo

kuvinaku kumalowerera mkulambira. Ali mkati molambira Katakwe amadzuka nkukapantha uthenga.

Akangotha kulalika kumakhala tsopano kupempherera odwala ndi osowa. Ikafika nthawi imeneyi akhiristu amakhamukira kutsogolo kukatula mavuto ndi nkhawa zawo kwa Katakwe. Ndipo nthawi zonse sipamalephera kukhala woperekera umboni kuti chozizwitsa chamuchitikira.

Maumboni ena amakhala ozizira monga, “Abusa sabata yatha mutandipempherera ndidakwera basi kupita mtauni. Ndidakafika mtauni kondakitala osandifunsa ndalamu.” Kapena “Ineyo mikodzo idandipola ndili mtauni koma ndidalibe ndalamu zolipirira chimbudzi. Ndidakakodza pamalo ena omwe adalemba kuti wokodza pano adzalipira chindapusa. Ine ndidakodza koma osandilipiritsa.”

Mpingo unkawomberabe mmanja maumboni ngati awa koma kumakhalanso maumboni ena ogwira mtima. “Mmenendimabwera, mutu umandiwawa koma mmene abusa andipempherera wasiyiratu.” Kapena “Abusa atangondipempherera basi andikweza ntchito.”

Maumboniwa amamveka kutali ndipo tchalitchi ya Katakwe nthawi zonse imakhala yodzadza. A Topitopi sadamuwuze Katakwe kuti akubwera. Adadikira tsiku la sabata ndipo adakalowa mwakachetechete. Ndisuti yawo yotuwa yomwe adavala, ma *usher* adangowaponya kumbuyo kwenikweni.

Koma ndi diso lake lakuthwa ngati la chiombankhangwa, Katakwe adawaona. Iye adadziwa kuti malume akewo adali mutchalitchimo kudzachita ukazitape. Adadziwa tsibweni akewo amadabwa kuti mmalo mwakugwa, zimatheka bwanji kuti mpingo wake womwe iye mwini adawatsimikizira kuti ndiwachinyengo uzikula?

Iye adanamizira kuti sadawaone. Adamwetulira akuganiza kuti kwa malume akewo, omwe adazolowera matchalitchi omwe obadwa mwatsopano amawatcha “amakolo”, padali povuta kudziwa kuti ali mtchalitchi. Magitala adali a ndombolo ndipo chodziwitsa kuti ndi nyimbo ya uzimu lidali dzina la Yesu. Ngakhale mavalidwe adali a chimtaira. Asungwana ndi amai adali mmadilesi aafupi kapena

adindadinda pomwe amuna adali mzovala izo nawonso amafuna.

Kutsogolo anyamata a *Praise Team* adali atakhwefula pomwe asungwana adali mma *miniskirt*. Mai wina wambuyo yaikulu ngati phiri ankavinitsa chiuno motenga moyo. Mkulu wina ankapalasa ngati gule wamkulu. Aliyense mtchalitchimo adali padansi yowopsa, ena akulutira, ena kuomba mmanja ena kuimba malikhweru.

Akulu ampingo adali akuvina kutsogolo. Naye Katakwe adavina moti apweteketse mtima tsibweni akewo. Iye amavina limodzi ndi Takondwa ndipo amati akamenyetsana manja kenaka amatembenuka nkuombetsana matako.

Itatha dansi, Katakwe adapita kuguwa. “Mpingo, mmanja mwa *Praise Team*. Ngati sitingavinire Ambuye, tidzavinira ndani? Tisaiwale mfumu Davide idavina moyaluka pamaso pa Yehova.”

Nthungululu zopolokozana ndi malikhweru komanso kuomba mmanja zidadzaza mutchalitchimo.

“Kutsutsana ndi wodzozedwa wa Yehova!” adakuwa Katakwe.

“Nkutsutsana ndi Yehova!” mpingo udayankha.

“Kutsutsana ndi *Miracle Maker!*”

“Nkutsutsana ndi Mulungu!”

“Wonyoza Prophet Katakwe!”

“Akunyoza Yehova!”

Iye adayamba nkulalika za chipulumutso. Panthawiyi anthu adangoti zii. Katakwe adaona apo ndi apo anthu akuwodzera. Oyasamula ngati nsomba zovuwulidwa mmadzi ndiye adalipo ambiri.

Kenaka uthenga udalowera kumadalitso omwe Mulungu amapereka. Mpingo wonse udayamba kuonetsa chidwi.

“Chuma chonse cha osakhulupirira ndi cha ife ana a Yehova. Koma kuti tichipeze tiyenera kubyala kaye. Baibulo limatiuza kuti yemwe adzabyala molira adzakolola mokondwera. Tsopano ndi nthawi yoti tibyale molira. Ndati motani?” adafunsa Katakwe.

“Molira!”

“Ndipo tidzakolola motani?”

“Mokondwa!”

“Mtchalitchi muno muli mbava, atsinzinantole omwe akumubera Mulungu. Pali anthu ena tikati choperekwa, simuperekwa. Chakhumi, simuperekwa. Zachifundo, simuperekwa. Zomangira tchalitchi, simuperekwa. Zosamalira abusa, simuperekwa.”

“Timasulen, abusa!” wina adakuwa.

“Mumaganiza kuti mukubisala. Koma simungabisale kudiso la wodzozedwa wa Yehova, ndikukudziwani. Kumbukirani kuti siliva ndi golide siwanu koma wa Yehova. Panopa ndikulengeza kwa yense yemwe saperekwa, matenda ndi imfa zisachoke pakhommo pake, matsoka ndi minyama zikhale gawo lake.”

“Inkani kwakuya abusa!”

“Panjapo tikugulitsa zinthu zomwe zikhoza kukuthandizani kupeza mdalitso wanu. Pali ena mumanyozera. Koma mupewa bwanji ngozi pamsewu ngati galimoto yanu ilibe sticker yathu yodalitsidwa? Matenda ndi matsoka akuchokani bwanji ngati simuvala zipewa zodalitsidwa zampingo wathu? Ma *T-shirt* ampingo wathu? *Anointed water* wampingo wathu? Nsalu zampingo wathu?”

“Wosagula akanthidwe!” wokuwa uja adateronso.

“Moto woopsa ukubwera kwa inu omwe simuperekwa zosamalira abusa. Simudziwa kuti nyumba yanga ndimalipira rent? Ndimayenera kulipira magetsi? Madzi? Galimoto yanga imafunika mafuta? Ndimayenera kuvala masuti oyenerera paudindo wanga ngati pulofeti? Mai busa amayenera kupita ku saluni?”

“Chedwanipo, munthu wa Mulungu!”

“Chonsecho mukadwala mumafuna ndidzakupempherereni. Pakhommo panu pakagwa maliro mumafuna ndidzakuyendetsereni mwambo. Ndikukudziwani omwe simusamalira abusa-tidzaona mukadzadwala, maliro akadzagwa pakhommo panu-mudzaone ngati ndidzapondepo.”

“*Download, man of God!*” adavomereza wokuwa uja. “*Libosaya mandrere liboshati khalapakatha.*”

“Ndiye musaganize kuti ndikukupemphani. Ine amandidyetsa ndi Mulungu. *I am a rich man.* Mutati muphatikize mtengo wazovala zomwe nonse mwavala, mtengo wake sungafike pazovala zomwe

ndavalazi.”

“*Dumba, mteweti!*” wina adakuwa mchitumbuka.

“Suti ndavalayi ndi Pierre Cardin, imported from France. Shatiyi ndi Armani, from Italy. Nsapatoyi ndi Gucci. Galimotoyo ili panjayo ndi latest Mercedes Benz. Ndili ndi nyumba, magalimoto ndi mabizinesi ambiri. Chaka chino ndikufuna kugula ndege,” adanyada Katakwe. “Amphawi a chabechabe, pa...manu, muli ndichani kuti mulimbane ndi wodzozedwa wa Yehova?”

“Timasuleni, abusa!”

“*Fools, imbeciles, dimwits,* ndalamu zanu ndi chiyani? Zitsiru, agalu, pa...panu; ndalamu zanu ndimazilandira pongofuna kuti mupeze mdalitso ndiye muzichitanso mtudzu!”

“*More fire, man of God!*”

“Ena tikati mupereke *seed* kapena chowinda simufuna kuperekwa koma ndinunso mumakhala patsogolo kusaka madalitso anga. Madalitso ali ngati mbewu, umakolola ndi momwe wafesera. Wofesa mowolowa manja amakolola zambirinso. Ndiyeno pano ndikufuna kugawa madalitso. *Who is ready to receive mdalitso wa Ambuye. If you are ready shout amen!*”

Ngati munthu mmodzi mpingo wonse udakuwa amen! Ena adaimirira, amuna akuimba malikhweru, amai akululutira. Achinyamata ankajowa ndi chisangalalo.

“Mdalitso woyamba ukupita kwa omwe akufuna kukhala a namatetule, mabigi, mabwana-omwe akufuna kuchoka pamlingo womwe ali kupita wina. Afike kutsogolo kuno ndi ma handede sauza-kashi kapena macheke, zowinda ayi ena simukwanitsa.”

Nkhope ya a Topitopi idaonetsa kudabwa kwambiri pomwe anthu a masuti awo, mabwana ndi madona, adathamangira kutsogoloko mokondwa ndi ndalamu kapena macheke kukalandira madalitso.

Kuchoka apo Katakwe adanka natsika ndi ma faifi sauza-kashi. Gulu lililonse linkapita malinga ndi mthumba mwawo komanso malonjezo a madalitso omwe Katakwe amalonjeza amapita nachepa mofanana ndi mlingo wa ndalamu zoperekedwazo.

Pomalizira Katakwe adati, “Tsopano inu omwe mwatsala mukhoza kubwera ndi kalikonse komwe muli nako mudzalandire

madalitso a chalala.”

Pamene magulu oyamba aja ankawagwira pamutu ndikuwapempherera, madalitso a gulu lomalizirali adali omwaza ngati mvula.

“Pomaliza, aliyense atenge ndalamaka penchi chomwe ali nacho monga mawotchi, macellphone, manekilesi, chilichonse kuti ndichidalitse.”

Anthu adatulutsa katundu yemwe adali naye.

“Zitukulireni kwa Mulungu,” anthu adazikweza. “Ndipo zili zokweza motero bweretsani zimene mwanyamulazo kutsogolo kuno,” anthu adafika nazo. “Ponyani mu basiketi umu kuti ndizidalitse.” Anthu adaziponya. “Ndayamika nonse omwe mwapereka kwa Ambuye, posachedwa Yehova akupatsani kuposera zomwe mwapereka. Tipemphere.”

Katakwe adafuna kuseka malinga ndi momwe malume ake amaonekera. Nkhope yaho siyimasiyana ndi ya munthu woonaerera munthu akuberedwa ponamizidwa.

Utatha mwambo wamapemphero, Katakwe adanamizira kuti sadawaone malume akewo. Iwo adakamupeza pagalimoto.

“Kodi ndi malume,” Katakwe adadzidzimuka dala. “Mukufika kumene?”

“*Haikona*,” malume adayankha kwinaku akumwetulira. “Ndafika kalekale moti mwambo wonse wamapemphero ndapanga nawo.”

Katakwe adawatsegulira chitseko cha galimoto yake. Tsibweniwo adakwera.

“Ndiye mwambo wamapemphero munawuona bwanji?” Katakwe adafunsa akuponya galimotoyo mugiya ulendo nkuyambika.

“*Hei, wena*, pamene paja sindanaonepo mapemphero koma umbanda; umachita kuja nkuba,” adatero a Topitopi.

“Kuba kwamtundu wanji? Pali amene ndinamupisa mthumba?”

“*Suka lapha, mfowethu*, kuba sikupisa m’thumba kokha,” adayankha a Topitopi. “Ndili ku Jubeki, wina wake adamumanga ndi mlandu wobera anzake powapusitsa. Mlandu wake ankati,” adadukiza kuti akumbukire, “ujeni...*theft by trick...nix*, ukupangayi ndi *theft by trick*.”

“Malume, mukukumbukira kuti nthawi ija ndimalalika za chipulumutso tchalitchi yonse inangoti zii?” Katakwe adafunsa ataima pa mphambano kudikira kuti alowe mumsewu.

“Eya,” adavomereza a Topitopi.

“Koma bwanji nditangoyamba kulalika za *prosperity*? ”

“Aibo, anthu amachita kuchemerera ngati mpira-chedwanipo, imanipo, abusa,” adatero a Topitopi moyeserera. “Koma tsono anthu abwinobwino aja amakhulupirira bwanji zomwe umanena zija?”

“Kaya! Tsono vuto ndi ndani?” adafunsa Katakwe.

A Topitopi sadayankhe.

“Akhirisituwo,” Katakwe adadziyankha. “Ife tikungowapatsa chimene akufuna, kuwauza zimene akufuna kumva.”

“Iwego udakamalalikabe zachipumulumutso...”

“Mupite ku mautumiki omwe amalalika za chipumulumutso, mukaone muli anthu angati,” adatsutsa Katakwe. “Anthu amafuna mautumiki achuma kapena machiritso. Ife tikulakwa pati kukwaniritsa zokhumba za akhirisitu athu?”

“Koma mumadziwa kuti zomwe mumachita zikuononga Chikhristu, zikupeputsa dzina la Yesu?”

“Motani?”

“Musamaganize kuti aliyense amapusitsidwa ndi zochita zanu,” adafotokoza a Topitopi. “Ena mumagwira mawere amai, matako ngakhale maliseche amene mtchalitchi. Ena kukamba zolaula. Kwa omwe siakhrisu akamaona mukuchita zinthu zachibwana ndi dzina la Yesu ngati mukuchita zisudzo kapena ndinu asing’anga, mukuganiza kuti amati chiyani za Chikhristu?”

Katakwe adalephera kuyankha. A Topitopi adapitirira. “Ngakhale mumatchula dzina la Yesu koma mumakhala mukuononga ulemu womwe udali ndi chimbedzo cha chikhrisu. Komanso anthu amayamba kukaika kuti ngati Yesuyo alipo, bwanji akulekerera anthu ngati inuyo kuti muzibera anthu?”

Mpata udapezeka ndipo Katakwe adalowa nayo galimoto ija mumsewu. Koma mmalo moyankha funso lomwe adafunsa malume akelo, iye adasinthia nkhani. “Malume, mukukumbukira

kuti ndidakuwuzani kuti anthuwa amapindula ndi mautumiki athuwa ngakhale amakhala abodza?”

“Hai, amapindula motani?”

“Chomwe ndidaona ine ndichoti munthu aliyense amafuna kupatsidwa chiyembekezo, ngakhale pamalo poti chiyembekezo palibe. Mwachitsanzo, ndikati anthu omwe akufuna ndiwapempherere kuti akhale mabwana abwere kutsogolo, ndimazizwa kuona anthu oti sadapite nkusukulu komwe akubwera, amaganiza kuti zikhoza kutheka bwanji?”

A Topitopi sadayankhe. Katakwe adapitirira. “Munaona anthu aja amapereka ndalamu; moti amaganiza kuti akhoza kugula madalitso kwa Mulungu ndi ndalamu? Koma amapereka chifukwa zimawapatsa chiyembekezo kuti akapereka seed tsogolo lawo likhala lowala—apeza kapena kukwezedwa pantchito, mabizinesi awo ayenda bwino. Ifeyo timawapatsa hope, chiyembekezo kuti mawa likhala labwino. Ndiye saluziratu.”

“Ukhoza kutero koma vuto ndiloti iwo aja amachita ndichikhulupiro chonse kuti ziyendadi iwe ukudziwa kuti ndibodza,” adaunikira a Topitopi.

Katakwe adamwetulira. “Ena mwamwayi zimawayenderadi.”

“Omwe sisiwayendera?”

“Kwanthawi yomwe amakhala akudikirira amakhala osangalala mpaka pomwe amazindikira kuti sisiyenda,” adayankha mosalabadira Katakwe.

“Koma iweyo sukuona kuti nkuchimwa kubera anthu osauka?” adalimbikira a Topitopi.

Katakwe adamwetulira. “Malume, vuto ndi dyera la anthuwa. Musaiwale paja mbuzi yagudu siyicedwa kukukumana ndi mpini. Mpiniwo ndine.”

“Komabe...”

“Tsbweni, ife tili ngati wa wachiona ndani. Anthu amapita wokha kukasewera wachiona ndani. Akaberedwa sipafunika kunena wanjugayo chifukwa sachita kuwaitana. Nafenso anthu amachita kutiputa dala.”

A Topitopi adagwedeza mutu wawo mosamvetsa.

“Malume, ndikupatseni chitsanzo chosavuta. Ndikadwala olo mai busa akadwala, akhrisitu omwewa amakatilipirira kuchipatala chodula chapulayiveti. Koma mukudziwa chomwe chimachitika iwo akadwala?”

Malume akewo adangomuponyera diso.

“Amabwera kuti ndiwapempherere. Bwanji sadzifunsa kuti chifukwa chani abusawa akadwala amapita kuchipatala pomwe iwo akadwala ndimangoti achira ndikawapempherera?”

A Topitopi sadathe kuperekanya yankho.

“Basi nkupusa kwawo. Kwa ine iyi ndi bizinesi. Mulungu ndi mpamba, anthu ndi makasitomala.”

“Komabe pena pake anthunu mukuonjeza...”

“Malume, tikamaonjeza ndiye zimakoka anthu kumene. Mudzaone mtumiki wochita zoonjeza ndiye amakoka anthu. Sindikukaika kuti kutsogolo kuno ndiyamba kuwadyetsa bibi anthu kuti azigoma nane.”





Chonyansa Pamalo Woyerā

Lero tipempherera amai omwe akusowa maanja, omwe maanja sakuyenda bwino komanso omwe nsalu yalekaleka sakuiona,” Katakwe adatero. “Lero nditsiku la mdalitso wanu.”

Amai adakhamukira kuguwa komwe adafola mzere. Katakwe adapemphera kwa kanthawi kenaka adapita pamzere wa amai uja. Dzanja lake lidafwamphuka ngati lilime la nanzikambe akamagwira ntchetché kudzagwa pabere la mai woyamba.

“Mzimu woyerwa akundiwa kuti mwana wanga ndiwe wouma ndipo sungabereke,” Katakwe adatero akugwiragwira bere lija. “Dyerekezi amayamwa bere lako.”

“Inkani kwakuya, *man of God*,” akhrisitu adakuwa.

Katakwe adachoka apo napita pa mai wina wambuyo yake ngati mbiya yamowa. Adamuzungulira maso ake atamatirira pambinayo. Kenaka adaigwira ngati akuiyeswa kulemera kwake.

“Usabisale,” iye adakuwa. “Ndikukuona ukubisa chiberekero mmbinayi.”

Padatsala asungwana awiri. Adapita kwa woyamba nayandikitsa nkhopre yake ndi ya msungwanayo ndikumuyang’ana kwa nthawi yitali. Mwadzidzidzi adamukumbatira msungwanayo nkuyamba kumupsopsona. Pomaliza adatembenuka nkukhala ngati akulavula.

“Ndachichotsa chiwanda chomwe chinali mchiberekero mwako,” Katakwe adalengeza.

Womalizira adali msunwana wokongola mochimwitsa wamsembe. Wamfupi, adali ndi nkhopre yobulungira ngati mwezi ndi maso akulu oyang’ana moleza. Dilesi lake lothina lidaika mndende mawere a njo ndi thupi loumbidwa ngati fano la mulungu wa chikondi.

Katakwe adamuyang’ana msungwanayo mwadyera, “Ndamuona pomwe woipayo akubisala. Mwana wanga, mulore wodzozedwa wa Yehova athane ndi vuto lako.”

“Amen!” adavomera msungwanayo.

Katakwe adayamba kumugwira msungwanayo ngati akupima china chake. Adamugwira mbuyo, kenaka mawere. Kenaka dzanja lake lidalowa mkati mwa siketi ya msungwanayo nkukagwira

maliseche ake.

“Ndakupeza,” iye adakuwa.

Nthawi yomweyo Katakwe adakhala ngati wamenyedwa ndi china chake. Adadzandira ndipo adakagwa pachipanda kukagwira guwa. Adagwedeza mutu kuonetsa kuti wabaizika.

“Lisondolo, likhethele,” adapemphera mmalilime. “Ndi njoka yokalamba ija, dyabulosi kachiwanda amene. Chemwali, ofunika mapemphero apadera. Mundipeze kuofesi masana ano.”

Mpingo udakuwa moonetsa kukhutitsidwa ndi zomwe amachita Katakwe. Masana, mapemphero atatha, msungwana uja adafika kudzamuona Katakwe muofesi ya tchalitchiyo.

“Chemwali, dyabulosi wamanga nthenje kumaso kwanu. Nchifukwa mmawa uja nditangogwira manthuyo ndinakhala ngati ndakanthidwa,” Katakwe adafotokoza.

Msungwanayo adaoneka wamantha. “Ndiye nditani, pulofeti?”

Katakwe adamuyang’ana msungwanayo ndi diso lamwala. “Chemwali, muli pabanja?”

“Ayi. Zibwenzi...”

“Zibwezi mumazipeza koma sizilimba,” Katakwe adamudula. “Ameneyo ndiye satanayo. Adaika temberero pa iweyo ndipo pano ndikukutsimikizira kuti banja sudzalipeza.”

Msungwanayo adagwada pamaso pa Katakwe. “Thandizeni, *man of God*. Banja ndikulifuna kwambiri.”

Katakwe adapemphera kwa kanthawi mmalilime. “Ambuye akuti zikhoza kutheka. Koma chofunika ndi chakuti ndikuthiren *anointed oil*.”

“I’m desperate, please help me, *man of God*,” adapempha msungwanayo ali chigwadire.

Katakwe adatulutsa botolo la *anointed oil*. “Mafuta amenewa ndi wofunika ndikapake mkatı mwenimweni mwa chiberekero. Vulani chemwali.”

Msungwanayo adavula. “Choyamba ndiyamwa kaye ziwanda zonse kuti zichoke kaye ndisadapake mafuta oyerawa.”

Katakwe adayamba kupsopsona malo osiyanasiyana a thupi la mtsikanayo. Kenaka adakhazikika popsopsona mawere kwinaku

akuyendetsa manja ake pathupi lamsungwanayo. Adapsopsona pamchombo kenaka kamwa lake nkukafika pamaliseche a buthulo.

Msungwanayo ankapuma mozama, mtima wake ukuthamanga malinga ndi zomwe amachita Katakwe. Kenaka Katakwe adavula zovala ndikutenga mafuta aja ndi kupaka chida chake chomwe chidali njo ngati mamba wokwiya.

“Tsopano ndikukapaka *anointed oil* m’chiberekero...”

Maganizo onse a Katakwe adali pazomwe amafuna kuchita ndi msungwanyo mwakuti adaiwala kuti sadakiye chitseko. Sadamve chitseko chikutseguka ndipo Takondwa akulowa.

“Chikatere?” Takondwa adamugenda ndi mawu.

Katakwe adaoneka ngati munthu wogwidwa akutamba. “Ndima... ndimafuna kuchotsa chiwanda...”

Ngakhale adali wokwiya, Takondwa adadziwa kuti nkhaniyi siimafunika kuti ikambidwe msungwana uja alipo. Adamuuza mtsikanayo avale ndipo azipita. “Ukakangoulula zomwe zimachitika muno Ambuye akakukantha,” adamuopseza msungwanayo.

Takondwa adamuomba Katakwe khofi. “Koma iwe ndiwe chitsiru eti! Iyi ndi bizinesi osati laisense yonyengera amai...”

“Wachikondi...”

Mbama ina idamutseka pakamwa. “Vuto la atumiki achinyengonu limakhala chiyani? Simufuna kuona munthu wamkazi ndi maso koma mumunyenje basi pomubwatika bodza mmaso.”

“Takondwa...”

“Kaya paja baibulo lidati chifukwa chake mukadzaona chonyansa chitaima pamalo oyera masiku omaliza ayandikira. Sungachite mantha kuti muno ndi mkachisi wa Mulungu?”

Katakwe adafuna kuyankha kuti zonse zomwe amachita mkachisimo zidali zachinyengo ndiye zimenezo zimasiyana bwanji. Koma mmalo mwake adangoti, “Tandimvetse, sikuti...”

“*Shut up. This should be the last time this kind of thing happens. We are here for money not kuvula amai. Zikadzangochitikanso ndidzakuyalutsa.*”

“Sindidzapanganso,” Katakwe adalonjeza.

“Good,” Takondwa adatero akupita kukakhoma pakhom.
“Tsopano ndikuonetsa zomwe amachita mkazi weniweni.”

Adalola kuti dilesi lake ligwe pansi. Mkati sadavale ndi kabudula
wamkati yemwe.





Ahabu ndi Yezeberi

Maso a Katakwe adalondola chiombankhangacho. Chidachoka mlengalenga ngati mwala wa legeni ndipo chidadzaikwatula nsombayo pamadzipo nkuwuluka nayo. Zonsezi zidachitika mkuthwanima kwa diso.

“Phunziro la moyo,” adatero Takondwa yemwe adagona pambali pa Katakwe. “Dziko lilibe chifundo ndi wofowoka-wamphamu ndiye amapulumuka.”

Awiriwa adagona pamchenga mmbali mwa nyanja ku Salima komwe adakasangalala. Mabotolo a mowa adali mbwe ngati masamba oyoyoka pansi pamtengo. Takondwa adatenga ndudu naitsomeka mosewera pakamwa pa Katakwe. Katakwe adailavula.

“Paja ine fodya yekha ayi,” iye adakana.

Takondwa adayatsa ndudu yake namuthira nawo utsi Katakwe. Kenaka adaika mutu wake pachifuwa cha Katakwe nayamba kusuta ndudu yakeyo.

Likisho, yemwe adali mu rumu yake, adatulukira ngati akuthawa njuchi zamalendewa zopanda mng’oma. “Tabwerani,” iye adawakodola.

Amati kati deru kaopsa mlenje; Katakwe adadzuka mwachangu namulondola Likisho. Takondwa adatola chitenje natsatira pambuyo.

Atalowa mu rumumo, Likisho adaloza pa TV.

“Apolisi ku Lilongwe agwira mkulu wa kampani ya Saracen International, James Kibo, pomuganizira kuti adapereka kontrakiti ku kampani ya Nagama Investments mwachinyengo,” wowerenga nkhani adatero.

Katakwe adadzidzimuka. “Jesus!”

Wowerenga nkhanayo adaptirira. “Nagama Investments, yomwe mwini wake ndi mai Yakobo, idalibe zoyiyenereza kulandira kontrakitiyo. Koma zikuoneka kuti a James Kibo adagwiritsa ntchito udindo wawo ngati mkulu wakampani kuti apereke kontrakitiyo. Padakali pano, a bungwe lofufuza za ziphuphu la *Anti Corruption Bureau...*”

Mtima wa Katakwe udadumpha. Akuluakulu adanena kuti chigwinjiri maliralira chidalondola msolo wankhwali; iye

adadziwa kuti nkhaniyo idakatha kugwetsa utumiki wake. Adayenera kuchitapo kanthu msanga ngati samafuna chinyengo chake chitumphukire poyer.

“Nkhani imeneyi tiyipange hando mosamala apo bi ikhoza kutiyalutsa,” Katakwe adabuwula.

“Aise, sukunama. Komanso ofunika tione kuti kutsogolo kuno titani chifukwa anthu ayamba kulankhula zokhudzana ndi utumiki wathuwu,” Likisho adatero.

Katakwe adaluma mulomo wammunsi. “Akuti chiyani?”

“Ayamba kusimba zochuluka. Akuti utumiki wathu ndiwafeki, kuti timangolalika zachuma osati zachipulumutso, tikugwiritsa ntchito utumiki wathu kubera anthu...zambiri.”

“Anthu ansanje amenewo,” adayankhirapo Takondwa. “Sakumva bwino kuti zikutiyyendera.”

“Chinanso, chiwaletsereni mai aja kumwa mtera sakuoneka bwino,” Likisho adatero. “Bwanji upeze njira yoti uwauze kuti ayambenso kumwa mankhwala?”

Katakwe adamuyang’ana mzakeyo modabwa. “Bwanawe, usaiwale kuti mpingo wathu udamangidwa pachinyengo. Kuti tingolowetsa kachilungamo, wonse ukhoza kutha.”

“Koma apa tikukamba za moyo wamunthu...” adaphereru Likisho.

“Kuti ndingovomera kuti ndidalakwitsa ndiye kuti anthu ayamba kukaikira zonse zomwe ndimanena,” adalimbikira Katakwe. “Usaiwale ndine mpulofeti. Mpulofeti salakwitsa, sangalakwitse. Panopa ndine kapolo wabodza langa lomwe.”

“Aise, ine zayamba kundikhudza’ adaulula Likisho. “Ukudziwa kuti anthu omwe timawanamiza amaika chikhulupiriro chawo chonse mwa ife?”

Katakwe adapuma mozama. “Bwanawe, ukukumbukira nkhani ya *Macbeth* ija tinkawerenga pa *English Literature* ku sekondale?”

“Yolembedwa ndi William Shakespeare?”

Katakwe adagwedeza mutu. “Apapa zafika paja *Macbeth* ankati: *I am in blood*

Stepped in so far that, should I wade no more,

Returning were as tedious as go o'ver."

"Ndiye uadowana momwe zidamuthera *Macbeth* chifukwa chosafuna kubwerera mmbuyo," Likisho adamukumbutsa Katakwe kwinaku akuponya diso lake pa Tokondwa mwadala.

Katakwe adadziwa kuti Takondwa, yemwe sadawerengepo nkhani ya *Macbeth*, sadadziwe tanthauzo la disolo. Kwakukulu, mkazi wa *Macbeth* ndiye adatsogolera kuti *Macbeth* agwe mmavuto okanika kutulukamo. Mwachangu adalikankhira kumbali ganizoli.

"Iwe ukuona kuti tikhoza kutani?" adafunsa Katakwe.

"Tiwauze anthu zowona."

Katakwe adaoneka wamantha. "Ukufuna atitenthe? Tapusitsa anthu angati? Tadya ndalama za anthu angati?"

Likisho adalibe choyankha. Katakwe adatembenukira kwa Takondwa. "Tamuza za chiombankhangha tinawona chija."

"Chinachoka mlengalenga nkugwira nsomba mnyanja," adalongosola Takondwa. "Ukuganiza kuti nsomba inasangalala kuti igwidwe?"

Likisho sadayankhe. Katakwe adadziwa maganizo omwe adali mwamzakeyo. Nthawi zambiri akakhala awiri, Likisho ankati ndimomwe Takondwa amakondera ndalama, samakaika kuti mtengo utakhala wabwino akhoza kugulitsa ngakhale mai ake.

"Ndimmene dziko lilili; wamphamvu amadyera wofowoka, wochenjera amadyera wopusa," adatambasula Takondwa.

"Ukuona, tiyenera kupidirira ndibodza," adatsendera Katakwe. "Nkhani ya mai Yakobo ndithana nayo sabata yomwe ino."

Motero nthawi yamapemphero a sabata yotsatira, adaimiritsa mai Yakobo kutsogolo.

"Mpingo, mukukumbukira kuti masiku apitawo maiwa adaima kutsogolo kuno kuchitira umboni pazomwe Mulungu adawachitira kuwapatsa kontrakiti?" Katakwe adafunsa.

Mpingo udavomera.

"Koma maiwa chisomo chokha sichidawawanire; adapitanso kuseri kukapereka chipuphu!"

Mokhumudwa, mpingo wonse udadzuma.

Katakwe adatembenukira kwa mai Yakobo. "Mai,

ndidakupemphererani ndipo Mulungu adapereka kontrakiti mmanja mwanu, chifukwa chiyani mudalola mdyerekezi akugwetseni mtchimo la chipuphu?”

“*Prophet*, ine sindikudziwa...”

Katakwe sadadikire kuti maiyo afotokoze. “Mai Yakobo, mpingo wathu ndiwoyera, sitilola *corruption*. Mukufuna munyazitse dzina loyera la Mulungu?”

“*Man of God*...”

Katakwe adakweza dzanja. “Ndikuuzeni Mrs. Yakobo, mutchalitchi muno sitisekerera uchimo ndipo *corruption* ndi mtundu umodzi wa uchimo.

Motero, takudulani mumpingo kuyambira lero.”

“*Prophet*...”

Koma Katakwe adawonetsa kuti wathana nawo. Adatembenukira kumpingo. “Mpingo, Mulungu safuna kuthandizidwa. Nonse mukudziwa chimene chidamuchitikira Uza atachirikiza likasa likufuna kugwa. Mulungu adamutani?”

“Adamukantha!” mpingo udayankha.

“Nzomwenso amafuna kuchita maiwa Mulungu atawadalitsa; kufuna kuthandizira popereka chipuphu. Ndiye monga Uza, Mulungu wawakantha pobweretsa poyer chinyengo chawo. Ndipo ife monga mpingo woyerwa wa Khristu tawadula kuyambira lero.”

Mpingo udawawowoza mai Yakobo ukukuwa, “*To go against the man of God is to go against God!*”

Atatha mapemphero, Likisho adakakumana ndi Katakwe ndi Takondwa kunyumba. “Bwanawe, palibe njira ina iliyonse yomwe tikhoza kuthandizira mai Yakobo? Ukudziwa alandidwa kontrakitiyi ndiye kuti aluza chilichonse. Alibe nyumba...”

Takondwa adamuyang’ana Likisho ndi diso lachiweruzo koma sadalankhulepo kanthu. Adangotulutsa ndudu yafodya nkuyamba kusuta.

“Atsogoleri, mukufuna kunena kuti tizivomereza uchimo mumpingo wathu uno?” Katakwe adafunsa mopanda chinzake.

“Ayi, koma...”

“Ndiye nkhaniyi yatha. Mrs. Yakobo tawadula mumpingo. Nkhosa zathu ziyenera kumvetsetsa kuti sitilola uchimo mtchalitchi mwathu.”

“Aise ineyo ndikuona ngati kuti monga mpingo tili ndi udindo wothandiza mai Yakobo. Adaperekwa nyumba ndi galimoto yawo kwa iwe...eeee... kumpingo komanso akhala akuima mwamphavu ndimpingo. Sitingawataye motere.”

“Sitingalolere mfundo zampingo kuti zipindidwe kaamba kachifundo...”

“Bwanawe ndikuonabe kuti tiyenera kuwathandiza. Ukudziwa kuti afunika ndalamza za lendi, zakudya, mafizi a ana ndi zina zotero. Komanso nkhani ya mankhwala ija tiyenera kuisova.”

“Aise, kodi ukufuna kundiuzu momwe ndiziyendetsera mpingo uno?”

Likisho adayang’ana Takondwa kuti mwina alowererepo. Koma mwana wamkazi zidaonetsa kuti sizimamukhudza. Adangopitilira kusuta fodya uja kwinaku akuimba nyimbo ya uzimu.

“Apa nkhaniyi yatha,” Katakwe adatero ataona kuti mzakeyo sadayankhe.

“Aise, ngati suwathandiza mai Yakobo ndiumirizidwa kuwulula chinyengo chomwe takhala tikuchita,” Likisho adatero motsimikiza.

“Atsogoleri, mukundiopseza?”

“Ayi, koma ndikuona kuti pameneba bodza lathuli tikhaza kutha nalo anthu. Ndiye zili ndi iwe,” Likisho adatero akuimirira.

“Atsogoleri, mukuiwala chinthu chimodzi.”

Likisho adaima pachitseko natembenuka. “Ndikuiwala chiyani?”

“1 Mbiri 16:22 ndi Masalimo 105:15,” Katakwe adayankha.

“Mavesi amenewa atani?”

“*To go against the man of God is to go against God,*” Katakwe adaunikira. “*Are you sure you want to go against God?*”

Likisho adayamuyang’ana Katakwe moderera. “Amwene, itayeni imeneyo, tonse tikudziwa kuti ndi slogan yongofuna kuti akhrisitu asamakutsutseni. *Going against you is not going against God.*”

“Ndine woimirira Mulungu padziko lapansi pano ndiye kulimbana ndi ine nchimodzimodzi kulimbana ndi Mulungu

yemwe adandidzoza kukhala mtumiki wake.”

“Wekha ukudziwa kuti siabusa onse amaitanidwa. Ena amadziyitana wokha monga iweyo. Ndiye atumiki odziyitananu nthawi zonse mumathawira kunena kuti baibulo lidati usanyoze wodzozedwa wanga. Wodzozedwa wake mbavanu?”

Katakwe adamuyang’ana mzakeyo mwachisoni. “*I hope you are aware of the consequences of going against God?*”

“*I’m going against you and not God!*”

“*I’m the anointed of God...*”

“Phu!” Likisho adalavulira pansi. “*Anointed of God!* Zamkutu!” Adatembenuka mwadzidzidzi nkutuluka m’chipindamo momenyetsa chitseko.

Katakwe adaimirira ndipo kudzera pazenera adamuyang’ana Likisho akupita ndinkhope yachisoni. Likisho adali mzake wapamtima koma tsopano amaopseza mpingo wake. Basi padali pofunika kuthana naye.

Takondwa adafika ndi tambula yamaimowa namupatsira Katakwe. Adaima kumbuyo kwake namusina mmapewa mwachikondi.

“*Sweetheart, ukudziwa kuti njoka saweta?*” adafunsa monong’ona mwana wamkazi.

Katakwe adavomera.

“Nthawi yakwana yofunika kumuphunzitsa Likisho kuti munthu suika mutu mkamwa mwa ng’ona nkuyembekeza kuti utuluka opanda zipsera,” adatero Takondwa. “*Let him face the wrath of God!*”

Kaya bwanji, china chake chidamupangitsa Katakwe tsembwe. Ndinkhope yake yopentedwa, zibangili zili mmanja monse, atavala sikeri yowonetsa nsonga zamatako, kwanthawi yoyamba Katakwe adakumbukira za Ahabu ndi Yezeberi. Mwachangu adalichotsa ganizo lakuti iye adali Ahabu pamene Takondwa adali Yezeberi. Sadayenera kuganiza mofowoka ngati Likisho.





Satana Aonetsa Nkhope

Pamene kumacha, mvula yomwe idakhala ikuopseza kuyambira mbandakucha, siyinayambebe. Komabe mabingu adapitirira kubangula ngati ng'oma zamganda. Mphezi ikang'anipa imakhala ngati bomba laphulika.

Katakwe adaima pakhomo la tchalitchi maso ake ali pa Likisho yemwe ankabwera atakwapatira ambulela. Likisho atafika, iye adatambasula manja ake nkumukumbatira. Akuchita izi, adaponya chithumwa mthumba la jekete la mzakeyo.

Adalowa mtchalitchi ndipo mwambo wamapemphero udayamba monga mwanthawi zonse. Itafika nthawi yolalika, Katakwe adadzuka ulendo kuguwa. Akuyandikira guwa adakhala ngati wamenyedwa ndipo adagwa pansi.

Adadzuka mwachangu. Adayamba kuponya zibakera kwinaku akupherera, akunjanja ngati muja amachitira munthu wankhonya. Zidaoneka kuti mdani wosaoneka yemwe amamenyana nayeyo amagonja mobwerera komwe kudakhala akulu ampingo. Zidaoneka kuti mdaniyo adalowa mwa Likisho.

“Usabisale, mdyerekezi, dzionetse wekha ndipo konzeka kupserera ndimoto wamzimu woyer!” Katakwe adaopseza akuloza Likisho.

Likisho adadzuka modabwa ngati munthu woti anali mtulo.

“Mdima sungaphatikizane ndi kuwala-ulula machimo ako, mwana wadyabulosi!”

“Abusa, chikuchitika nchiyani?”

“Ndikuti ulula machimo ako!”

“Machimo anga?”

“Eya-umfiti, matsenga, kutamba!”

“Sindine mfiti...”

“Ndakuona muuzimu utasanduka chiwanda ndipo unandipanga attack.”

“Bodza!”

“Ukunena Ambuye wabodza? Tiyeni tione pakati pa iwe ndi Ambuye kuti wabodza ndani. Tulutsa chithumwa chomwe chili mthumba mwako!”

Bata lidagwa mtchalitchimo anthu akudabwa kuti chikuchitika

nchiyani, maso onse atamatirira pazomwe zimachitika kutsogoloko.

Likisho adalowetsa dzanja mjekete lake. "Mulungu siwabodza koma..." mawu ake adadukira kukhosu pomwe dzanja lake lidatulutsa chithumwa.

Aaah! adamveka m'tchalitchimo.

Katakwe adagwiritsa ntchito dangali tsopano. Adanunkhiza mmwamba muja amachitira galu. Mphenzi idang'anima. "Ndikumva fungo, fungo lamoto, inde ndi mwini tchimo, njoka ija yokalamba, Lusifala."

Adatembenukira kwa Likisho. "*Speak, satan, who are you?*"

"Abusa, ndatopa ndizochita zanu, lero ndiwulula kumpingo zimene mumachita!"

Katakwe adamugwira Likisho mmapewa ndipo monong'ona adati, "Munthu woganiza sulimbana ndi ng'ona mmadzi; watch me and learn, fool!" Kenaka adakuwa. "*Ma usher, gwirani mdyerekezi.*"

Ma usher adamuwakha Likisho, nkumupindira manja kumbuyo ngati amuveka nyakula. Katakwe adavula jekete ndikutembenukira kumpingo. "Pano pali chiwanda choopsa koma lero tithana nacho," iye adalengeza akupinda shati.

Mpingo onse udadzuka. "Chiphwanyeni, munthu wa Mulungu!"

"Chithireni moto wamzimu woyer!"

Katakwe adayamba kumumenya Likisho kwinaku akukuwa "*Confess, devil! Confess!* Adamumenya zibakera mmimba ndi kumuthira makofi."

"*Yes, I confess!*"

Katakwe adamumenya mmimba. "*The church can't hear you, demon, you confess to what?*"

"*I am a witch.*"

Likisho adalandira theche la mphechepeche. "Mpingo sukumva, ndiwe ndani?"

"*Mfiti!*"

Katakwe adawerama nanong'ona kukhutu kwa Likisho. "Uwfotokozere mpingo kuti mdyerekezi adakutuma kuti udzaononge utumiki wanga ponena mabodza." Koma mokuwa adati, "*What was your mission in this church, demon?*"

“I wanted to destroy the Prophet and his Ministry by spreading lies about him.”

Katakwe adatsitsanso mawu. “*You have seen what I am capable of doing to protect my ministry; you say anything about this, we will kill you, understand.*” Likisho adagwedeza mutu kuonetsa kuvomera. “*And I don’t want to see you in this church again, understand?*” Likisho adagwedezanso mutu.

Mokweza Katakwe adati, “*If you are a witch, demon then this is the wrong place to be. We shall expose you and burn you with Holy Ghost fire!*”

Mkuwe wampingo woti, “*Fire! Fire! Fire...*” udamizidwa mkulira kwa mabingu omwe adabangula ndikubangula ngati mkuwe wa agalu achisika.





Chiwanda Choopsa

Malotowo adayamba tsiku lomwe adalengeza manthu wamsonkhano wachitsitsimutsowo. Malotowo amakhala amodzimodzi. Mmalotomo Katakwe ankachotsa ziwanda. Mai Yakobo ankakhala mgulu la anthu omwe ankachotsedwa ziwandazo. Ikafika nthawi yoti amuchotse, mai Yakobo ankasanduka chiwanda choopsa-chimzukwa cha mutu waukulu, maso otuzuka ndi zala zosongoka ngati za nyalugwe.

“Siungatitulutse Katakwe chifukwa ife ndife mbuye wako,” chiwandacho chinkatero mmawu a besi ngati bemberezi.

“*You are not my master, demon. Out!*” Katakwe ankakuwa mwamantha. “I am a man of God!”

Chiwandacho chinkaseka. “Sindiwe munthu wa Mulungu. Munthu wa Mulungu angapange zomwe udandipanga ine?”

“*Liar, I am a Prophet of God.*”

“Iweyo ndiwe woipa kuposa mbava. Monga mphutsi ukulemera pamavuto a odwala, osauka, ofooka ndiye nkumadzitcha mpulofeti?”

“*You are a liar. Out of her body!*”

“Onetsa, ulemu kwa mbuye wako. Sangalaliratu ndi chuma chadziko lapansi koma dziwa kuti ukadzafa mzimu wako ndi wa ine Dyabulosi.”

Katakwe ankadzuka ndi mkuwe, thupi lonse litanyowa ndi thukuta. Poyamba amangoti ndi maloto, koma ataona akupitirira, adayamba kuchita mantha.

“Ndimaganiza kuti tipange khango *crusade imeneyi*,” iye adamuwuza Takondwa, yemwe adagona pambali pake.

“Ayi, *crusade imeneyi* siyingapangidwe cancel. Taononga kale ndalamu zambiri zokonzekera komanso pali nduna ndi olemekezeza ena omwe atsimikiza kale kuti adzakhalapo.”

“Sindikudziwa, koma ndikuona ngati tikadapanga *cancel*.”

Takondwa adatulutsa ndudu yafodya nayatsa. “Katakwe, ndiwe *professional*, usalolere kuti loto lopusa likuope.”

“Koma nanga zitakhala zoona kuti Mulungu alipodi?”

Takondwa adaseka. “Sindikukhulupirira kuti ndiwe ukunena zimenezi. Mulungu sangakhale kuti alipodi chifukwa ngakhale

satana kulibe.”

“Koma nanga titakhala kuti tikulakwitsa?”

“Sitikulakwitsa. Tapusitsa anthu angati? Tadyera anthu angati? Adakakhala kuti Mulungu alipo, adakalola kuti tizichita zomwe timachitazi? Zomwe tidachita kwa Mrs. Yakobo?” adamulimbitsa mtima Takondwa.

“Likisho tidamuchititsa manyazi mutchalitchi, kuguwa kumene, bwanji Yesu sadalowererepo?”

Katakwe adalibe yankho.

“Chifukwa Mulungu kulibe,” adadziyankha Takondwa. “Chipembedzo ndi nthano chabe yomwe idapekedwa kuphunzitsa anthu chikhaliidwe. Mulungu kuphunzitsa zabwino ndi satana kuopseza anthu kuti asamachite zoipa.”

“Panopa sindikudziwa ngati chipembedzo ndi nthano kapena chiyani. Kuipa komwe demoniyo amalankhula ndayamba kukumva kukuyenda mmagazi mwanga ngati mtsinje. Chodabwitsa ndayamba kuona ngati zomwe timachita nzoipa.”

Takondwa adadzuka napita kukatsegula firiji. Adatenga mowa nkuthira m’matambula awiri. Adatenga imodzi nkumupatsa Katakwe.

“Imwa pang’ono, ukhala bwino. Pali mapulofeti ambiri amene akunamiza anthu kuposa ifeyo, chifukwa chiyani Mulungu sakuwakantha?” adamuchirimika Takondwa. “Mulungu kulibe.”

Mauwa adamulimbikitsa Katakwe. Adagubula mowa uja. “Wandilimbikitsa, sitipanga *cancel*.”

Takondwa adadzuka namukhalira pamimba. “Ameneyu ndiye Katakwe amene ndimamudziwa,” adawerama namupsopsona Katakwe pakamwa. “Ikamatha *crusade* imeneyi tikhala anthu olemera kwambiri.”





Nkhope ya Mulungu

Mapempherowo adachitikira muholo yaikulu kwambiri yomwe idakongoletsedwa mwapamwamba. Fumbi la anthu lomwe lidafika lidadzaza holoyo mpaka kusefukira kunja.

Katakwe adawala ngati mngelo. Chilichonse chomwe adavala chidali choyer. Suti yake yokhala ndi jekete lalitali lolekeza mmawondo inkanyezimira ngati golide pamene nsapato zake zidali zoyer. Tsitsi lake lambiri lojelula linkaoneka mosasiyana ndi la mbusa uja wa mu filimu ya *Eddie Murphy* yotchedwa *Coming to America*.

Ndipo zodabwitsa zidachitikadi. Osayenda adayenda. Osamva adamva. Akhungu adaona. Monga mwa nthawi zonse onse omwe adachirawo adali anthu oti Katakwe adapangana nawo.

Ochirawo adachitira maumboni. Padali amai ndi abambo oti munthu sangawaganizire kuti akhoza kumachita chinyengo chotere. Koma paja aliyense ali ndimtengo wake; atalonjezedwa ndalamala zambiri, adakatha kukana bwanji?

Mwambo wopempherera anthu udali utatha pomwe msungwanayo adawonekera.

“*Prophet*, ndikufuna kuyenda!”

Katakwe adaponya maso ake komwe kudachokera mawuwo. Adali msungwana wa zaka zozungurira khumi ndi zisanu ndipo adali pa whilutcheya. Miyendo yake imao netseratu kuti idali yolumala zenizeni.

“*Man of God*, ndikudziwa Yesu andichiza lero,” adatero msungwanayo.

Thukuta lidagwa pankhope ya Katakwe. Mtsikanayo adali wolumaladi. Iye adalibe mphamvu ina iliyonse yamachiritso. Apanga bwanji? Adamuyang’ana Takondwa; naye adangoti kukamwa kakasi.

Msungwana uja adafika kutsogolo.

“Wodzozedwa wa Yehova, paja nthawi zonse mumati Yesu salephera ndipo ndikudziwa lero andichiza.”

Bata lidagwa m’tchalitchimo muja kunja kumachitira kukati kugwa mvula yamkuntho, maso onse ali pa Katakwe. Kuchokera pomwe adakhala, Takondwa adapereka chizindikiro chomuletsa

Katakwe kuti asachitepo kanthu.

Koma Katakwe adakazemba bwanji maso onse ali pa iye? Adamasula kolala yake yaubusa nagwada pambali pamsungwanayo.

“Sungamvetsetse, mwana wanga, koma palibe chomwe ndingakuchitire.”

“*Prophet*, mumanena nthawi zonse kuti sindinu mumachiza koma Yesu.

Ineyo ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti Yesu andichiza lero.”

Katakwe adapuma mozama. “Mwana wanga, Mulungu andikhululukire; munthune ndilibe mphamvu ina iliyonse yamachiritso.”

“Ndikudziwa, prophet kuti simuchirtsu ndinu koma Yesu ndipo monga mumanena Yesu ndiyemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zosatha ndipo salephera motero lero andichirtsu,” adalimbikira msungwanayo.

Misozi idadzaza mmaso mwa Katakwe. Iye adaona kuti mwanayo adali ndi chikhulupiro chonse kuti kudzera mwa iyeyo achira. Iye adadzimvera chisoni pomwe adazindikira chipsinjo chomwe chinyengo chake chimaika mwa anthu omwe amamukhulupirira.

Adagwada nalemba chizindikiro chamtanda ngati mkatolika. “Ambuye Yesu ndikhululukireni chifukwa ndakuchimwirani....”

Anadabwa pomwe mpingo wonse udabuka phokoso lachisangalalo. Katakwe adaptirira kulira; sindiye kuti anthuwo amamuseka? Koma anadabwa akugwedededwa paphewa.

Potsegula maso adazizwa kuti adali msungwana uja. Adali atachira, miyendo itawongoka ngati kuti sadali wopuwala.

“*I can walk! I can walk!*” msungwanayo adakuwa akujowa mosangalala. “Zikomo kwambiri Ambuye Yesu!”

Mpingo wonse udalinso ukujowa, kukondwera ndi mphamvu ya Ambuye koma Katakwe ndi Takondwa sadajowe nawo. Takondwa adali atakomoka ndimantha pomwe Katakwe adakhala pansi, mutu uli mmanja, nkhope ili chithunzithunzi chodabwa chosakanikira ndi nkhwawa.

“Ndizoona Yesu amachiritsadi,” Katakwe, misozi ili mbwembwembwe mmaso, adavomereza monga muja mkulu wa asilikali achiroma adavomerezera kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu nthawi ija Yesu amatsirizika pamtanda.

Zidachitikazo zidamutsimikizira kuti Mulungu alipodi ndipo amachitadi zozizwitsa. Koma nkhawa yake idali yakuti kodi ndi chinyengo chake chija, zimuthera bwanji?



M'dzina la Yesu

Masiku ano, mautumiki ndi bizinesi yotentha kwa mapulofeti onyenga amene akugwiritsa ntchito dzina la Yesu kupusitsira anthu. Kupatula kupeputsa dzina la Yesu ngati choseweretsa, mautumiki amenewa amapereka chiyembekezo chabodza chimene mathero ake chimabweretsa kuganiza kolakwika kofuna kupeza zinthu mosakhetsara thukuta komanso imfa kwa odwala matenda omwe ndi ochizika kuchipatala.

Munkhaniyi, mbali imodzi kuli mbusa Kaduya yemwe amakhulupirira kuti ndi Mulungu chili chonse ndichotheke koma panthawi yake yoikika. Mbali inayi, kuli Katakwe amene sakhalupirira kuti Mulungu amachita zozizwitsa. Kwa iye, amakhulupirira kuti zozizwa zonse zimene atumiki a Mulungu amapanga mdzina la Yesu, ndi zachinyengo zongofuna kupusitsa anthu ndi cholinga chowadyera.

Motero, mbusa Kaduya atadalitsika mwapadera, naye Katakwe adayambitsa utumiki wake ngati chida chopangira ndalamu. Amati utumiki wachinyengo supita patsogolo, koma utumiki wa Katakwe udapita patali kwambiri. Funso nkukhala; chifukwa chiyani anthu amakhamukira ku mautumiki oonekeratu kuti ndiachinyengo?

Nthano za Katakwe zimatuluka sabata iliyonse m'nyuzipepala ya Weekend Nation. Bukuli ndi nthano imodzi yaitali.

LAWRENCE KADZITCHE

A Lawrence Kadzitche adachita maphunziro awo ku Magawa Secondary School, nakapitiriza ku Polytechnic. Ngakhale amagwira ntchito zina, chidwi chawo kwambiri chili pakulemba nkhani zopeka. Ili ndi buku lawo lachisanu. Mabuku awo ena ndi Katakwe Kutauni, Katakwe Zaka 10, Katakwe Kumudzi ndi Slay Queen.



9 7 5 9 9 9 0 8 9 7 3 0 2